Language L.45

# Chichewa Malawi

مركز المعلومات الإسلامي
Islamic Information Center
للتعريف بالإسلام

Version Date: 2025




Part of the

ISLAMIC e-LIBRARY

Learn more about Islam with our informative and educational materials, translated to over 50+ languages

@islamicicdxb

CONTENTS


MAU OTSEGULIRA OFOTOKOZA CHISILAMU

MTUMIKI MUHAMMAD
MTENDERE UKHALE PA IYE

YESU: MTHENGA WA MULUNGU (ALLAH)

MULUNGU M'CHISILAMU

KORANI

KODI CHOLINGA CHA MOYO NDI CHIANI?

KUCHIMVA MOLAKWIKA CHISILAMU

UFULU WA AKAZI M'CHISILAMU

KUSAKHULUPIRIRA MLENGI
M'KAYANG'ANIDWE KA CHISILAMU

ZOZIZWITSA ZASAYANSI MU QUR'AN


# MAU OTSEGULIRA OFOTOKOZA CHISILAMU


CHICHEWA (MALAWI) (01/11) نبذة عن الإسلام FREE COPY


NJIRA YA MOYO YOTHEKA KUIGWIRITSIRA NTCHITO KOMANSO YAPAKATIKATI

UBALE WAMPHAMVU KOMANSO WACHINDUNJI NDI MULUNGU (ALLAH)

KAMVETSETSEDWE KOLONDOLA NDI KOMVEKA BWINO KOKHUDZA MULUNGU (ALLAH)

UTHENGA WOGWIRIZANA NDI NYENGO ILIYONSE NDI MALO ALIWONSE


جمعية دار البر
Dar Al Ber Society
www.daralber.ae

الإمارات
THE EMIRATES

Your Path To Peace..

مركز المعلومات الإسلامي
Islamic Information Center
للتعريف بالإسلام

تصريح رقم:
(2017/139)


دائرة الشؤون الإسلامية والعمل الخيري
Islamic Affairs & Charitable Activities Department

www.islamicic.com

CONTENTS


























# KODI CHISILAMU NDICHIANI?

Chisilamu chimatanthauza kuti ukukhulupirire mwa Mulungu Mmodzi Wowona (yemwe amatchedwa "Allah" pachiarabu), ndi kuti umpembedze Iye Yekha, ndi kuti ukhulupirire mwa Mneneri Muhammad (madalitso ndi mtendere zikhale pa iye) kuti ndi womaliza wa atumiki ake.

Pafupifupi munthu m'modzi mwa anthu anai aliwonse ndi msilamu (chiwerengero chomwe chikuimira 23 peresenti), chiwerengero chawo chimapitirira mabiliyoni awiri.

Anthu otsatira Chisilamu amadziwika ndi dzina lakuti asilamu, ndipo angathe kukhala ochokera mu mtundu uliwonse kapena fuko lililonse.

# CHIKHULUPIRIRO NDI CHIPHUNZITSO

Mulungu (Allah) akutiitanira kuti timukhulupirire kupyolera mu zisonyezo zake, ndipo kumzindikira kumeneku wakupanga kukhala gawo la udindo wathu. Zimenezi ndi gawo la mayesero a moyo uno. Popanda njira yoyenera ndiye kuti ngakhale maphunziro atachuluka bwanji sangampangitse munthu kukhala wokhulupirira.

- ✔ Kusakhala ndi tsankho ndi kukhala ndi nzeru zotseguka
- ✔ Kudzichepetsa ndi kuyeretsa zolinga
- ✔ Kulingalira za cholinga cha kupezeka kwathu padziko
- ✔ Kuzindikira/kulandira zisonyezo za Mulungu (Allah)

- ✘ Kudziikira zitchingo/maganizo olakwika ndicholinga chakuti asakhulupirire
- ✘ Kunyada ndi kudzikuza
- ✘ Kungokhazikika pa kulingalira za mdziko
- ✘ Kuchikana chilichonse ponena kuti chilibe tanthauzo lilionse

# CHIFUKWA CHOYAMBA: CHIYAMBI CHA CHILENGEDWE (DZIKO)

Chifukwa choyamba chochititsa kuti tikhulupiririre mwa Mulungu (Allah) chikukhudzana ndi kulingalira chiyambi cha chilengedwe (dziko).

**Kodi chinabwera bwanji ndi kukhala chinthu chopezeka?**

- ✘ Kodi chinachokera mu kusapezeka? Yankho nlakuti palibe chinthu chomwe chimachokera mu kusapezeka. Ndiye kuti mwachidziwikire sichoncho.
- ✘ Kodi chinadzilenga chokha? Ayi, kuyankhula choncho ndi kopanda nzeru, chifukwa zili ngati kunena kuti mai anadzibala wokha.
- ✘ Kodi chinali chopezeka nthawi zonse? Ayi, sayansi imayankhula monenetsa kuti chilengedwechi chili ndi chiyambi chake.
- ✔ Kodi chinachita kulengedwa? Inde. Asilamu amakhulupirira kuti wina wake yemwe ali Sali gawo la chilengedwechi ndiyemwe analenga chilengedwe, yemwe ndi Mulungu Wolenga.

**Koma nanga ndindani yemwe adamulenga Mulungu (Allah)?**

Mulungu (Allah) sadalengedwe. Mosiyana ndi dziko pamodzi ndi chilengedwe chonse, Mulungu (Allah) Ndiye Woyamba yemwe patsogolo pake palibe chilichonse, ndiponso Ndiwomaliza yemwe pambuyo pake palibe chilichonse.

CONTENTS

































# CHIFUKWA CHACHIWIRI: KULONGOSOLEDWA BWINO KWA DZIKO

Chifukwa china chophweka chochititsa kuti tikhulupirire mwa Mulungu (Allah) ndicho kulingalira za kulongosoledwa bwino ndi kusanjidwa bwino kwa dziko, pogwiritsira ntchito mfundo zanzeru zotsatirazi:

1. Chinthu chilichonse chosanjidwa bwino chimasonyeza kuti pali luntha.

2. Ndondomeko ya dongosolo la dzuwa (Solar System) ndi yosanjidwa bwino zedi kudzera mu ndondomeko komanso malamuro ndi kakhalidwe kovuta kukamvetsetsa masanjidwe ake.

3. Kusanjidwa bwino kwa zinthu m'dziko lathuli kukusonyeza luntha la Mlengi.

Ndondomeko zambiri zomwe zili m'dzikoli zimasonyeza poyera kuti izozo zinakonzedwa mwapaderadera kuti zithandizire moyo. Ndipo ngati mapimidwe amenewa atangosintha pang'ono chabe kuchoka momwe alili, ndiye kuti moyo sungakhale wotheka. Ndipo zina mwa zitsanzo za zimenezi ndi;

- Ozone layer
- Makulidwe a mphipi ya nthaka
- Mpweya wa okosijini m'malengalenga
- Mtunda womwe ulipo kuchoka pamene pali dzuwa
- Makulidwe osiyana pakati pa dzuwa ndi dziko lino, ndi mwezi

Kodi zingatheke chidziko chachikulu komanso chovuta kuchimvetsa ngati chimenechi kuti chiwumbike mwangozi popanda uyang'aniri uliwonse? Nkofunikira kudziwa kuti Chisilamu chimalimbikitsa ufufuzi wa sayansi ndi kulingalira. Sayansi imatenga gawo lothandizira kuzifotokera zisonyezo zankhaninkhani zimene Mulungu (Allah) adazimwaza mu zolengedwa zake, ndiponso lothandizira kumvetsa bwinobwino kutha kwake ndi luntha lake.

# CHIFUKWA CHACHITATU: CHIVUMBULUTSO – KORANI

Korani imatengedwa kuti ndi umboni wamphamvu wosonyeza kuti Mulungu (Allah) alipodi, ndipo siingafanane ndi chilichonse m'kasnjidwe kake, ndi luntha lake, ndi chiongoko chake, ndi kayankhulidwe kake komveka bwino, ndi kusiyana kwake ndi mau ena onse pamene oiwerenga akuiwerenga.

- Mulibe zolakwika zilizonse kapena kudzitsutsa kwa mtundu uliwonse
- Ili ndi kafotokozedwe kolondola ndi komveka bwino kokhudza Mulungu (Allah).
- Ndi mapeto a kukongola kwa chiyankhulo chachiarabu
- Idavumbulutsidwa kwa Mneneri Muhammad (madalitso ndi mtendere zikhale pa iye) yemwe adali wosatha kulemba ndi kuwerenga
- Ndiyotetezeka – mulibemo kusinthidwa kulikonse pambuyo podutsa zaka 1400
- Kuzindikiri kwakuya kokhudza chikhalidwe cha munthu
- Anthu mamiliyoni adailoweza pamtima
- Ili ndi nkhani zotsimikizika za sayansi zimene anthu sanali kuzizindikira mu nthawi imeneyo.

*"Ndipo m'nthaka muli zizindkiro kwa okhulupirira (zosonyeza kuti Mulungu (Allah) alipo). Ndi mwa inu nomwe, kodi simukuona?"*

Qur'an 51:20-21

CONTENTS

































# KODI MULUNGU (ALLAH) NDI NDANI?

Chimodzi mwa zokongola zikuluzikulu za Chisilamu ndi chakuti chimavomereza kukwanira kwachikwanekwane, ndi ukulu, ndi umodzi wa Mulungu (Allah) popanda kuchotsera kulikonse.

- Mulungu (Allah) Ndimmodzi komanso Wayekha, ndipo alibe aliyense wofanana naye kapena athandizi kapena ana.
- Mulungu (Allah) – ulemerero wake utukuke – ndi woyenera kupembedzedwa payekha komanso mwachindunji, (popanda akhalapakati aliwonse).
- Mulungu (Allah) Ndiwokwanira ndipo alibe zilema kapena chofowoka chilichonse.
- Mulungu (Allah) Ndiwachifundo – amadziwa kuti ifeyo ndife osakwanira ndi kuti timachita machimo, koma ngakhale zili choncho makiyi ndiwo kuvomereza mwachowonadi zolakwitsa zathu ndi kupempha chikhululuko.
- Mulungu (Allah) salowa mu zolengedwa zake ndiponso palibe wina aliyense yemwe amatenga nawo gawo lililonse mu mbiri zake zaumulungu.

Pamene tikuyesayesa kufuna kumvetsetsa za chikhulupilro cha Mulungu (Allah) m'chisilamu, n'kofunikira kukamba za chikhalidwe cha Yesu, malingana ndi chisokonezo komanso zonenedwa zofalikira zomwe zilipo zokhudza chikhalidwe cha m'mene iye aliri.

M'chisilamu timakhulupirira mwa Yesu kumbali yoti iye ndi Mneneri komanso Mtumiki wolemekezeka wochokera kwa Mulungu (Allah), koma kuti Asilamu samupembedza chifukwa chakuti kupembedzedwa ndi kwa Mulungu Yekha yemwe adamulenga Yesu ndi chilichonse chopezeka. Kwa ichi, chikhulupiriro chonena kuti Yesu ndiye Mulungu, kapena mwana wa Mulungu, kapena gawo la utatu wa Mulungu, chikutsutsana kotherathu ndi ziphunzitso zomveka bwino zokhudza Mulungu (Allah) m'chisilamu.

**Ngati Yesu ali Mulungu, ndiye anali kumulambira ndani?**

Pali zitsanzo zambirimbiri m'ziphunzitso za Chikhirisitu zokhudza Yesu zomwe zimaonetsa kuti iye anali kulankhula ndi kuchita ngati kuti Mulungu ndi chinthu china cholekana ndi iye (Yesuyo). Mwachitsanzo, Yesu anali kupemphera kwa Mulungu.

**Zingatheke bwanji Mulungu kukhala wokwanira ndi wosakwanira nthawi imodzi?**

Yesu anabadwa, ndiponso anadya, ndiponso anagona, ndipo kudziwa kwake kunali ndi malire, zonsezi ndi mbiri zimene sizimuyenera Mulungu (Allah). Mulungu (Allah) ali ndi mbiri za chikwanekwane, pomwe munthu ndi otsutsana ndi zimenezo.

**Kodi liwu lakuti "mwana wa Mulungu" limatanthauza chiani kwenikweni?**

Tikupeza kuti mau akuti "mwana wa Mulungu" malingana ndi mabuku akale a Baibulo amagwiritsidwa ntchito pofuna kutanthauza munthu woyera mtima, ndipo zimenezi zidagwiritsidwa ntchito kwa anthu ambiri, osati kwa Yesu yekha ayi. Mulungu (Allah) ali kutali zedi ndi mfundo yonena kuti iye ali ndi mwana wakuthupi kapena weniweni.

**Ngati Mulungu ali wakutha kuchita chinthu chilichonse ndiye n'chifukwa chiani sangathe kusanduka munthu?**

Mulungu (Allah) nthawi zonse amasunga mbiri zachikwanekwane ndipo sangachite chinthu chilichonse chomwe chingaononge kukwanira kwake. Malingana ndi tanthauzo la kukhala mulungu, "Mulungu" samachita ntchito zosakhala za umulungu. Kwa ichi, ngati Mulungu angasanduke munthu ndi kudziveka mbiri za umunthu ndiye kuti popanda kukaika sangakhalenso mulungu pambuyo pa zimenezo.

CONTENTS

































## ATUMWI AMBIRI

Aneneri ndi Atumiki ambiri monga Adamu, Nowa, Abrahamu, Mose, Yesu ndi Muhammad ndi ena (madalitso ndi mtendere zikhale pa iwo), onsewo;

## UTHENGA UMODZI

- Amatsindika pankhani ya Mulungu Mmodzi, ndipo amaikana milungu yambirimbiri ndi zikhulupiriro zopotoka.
- Amafotokoza mwamvemvemve njira yomupembedzera Mulungu (Allah).
- Amakhala chitsanzo chabwino cha ungwiro ndi makhalidwe abwino.
- Amafotokoza malipiro a kumumvera Mulungu (omwe ndi munda wa mtendere)
- Amachenjeza za chilango cha anthu onyozera malamuro a Mulungu (chomwe ndi moto wa Gahena).

Mulungu (Allah) wakhala akutumiza Aneneri kumtundu uliwonse m'nyengo zosiyanasiyana ndi uthenga umodzi waukulu wakuti – ampembedze Mulungu Mmodzi Yekha. Koma ngakhale kuti asilamu amawakonda Aneneri onse ndi kuwalemekeza chabe kuti iwo samawapembedza kapena kuwapatsa umulungu, chifukwa chakuti umulungu ndi ufulu wa Mulungu (Allah) Yekha basi.

# CHOLINGA CHA MOYO

Mulungu (Allah) Waluntha sadatilenge kuti tizingoyumbayumba popanda cholinga chilichonse, kapena kuti tingokwaniritsa zilakolako zathu zachilengedwe basi. Koma tili ndi cholinga chapamwamba zedi, chomwe ndi "kukhulupirira mwa Mulungu (Allah) ndi kumpembedza Iye Yekha, ndi kuti tikhale moyo wathu mogwirizana ndi malamulo ake. Chiwongoko chimenechi ndi chimene chimabweretsa moyo wosangalala ndi wopambana mu mbali zonse.

Ndimbali imodzi ya luntha la Mulungu (Allah) lopanda malire kuti Iye adatilenga ndi kutipatsa mwayi wa kumudziwa, ndi kuwudziwa moyo wathu, ndi kupanga zisankho zathu zapadera.

Chisilamu ndi njira yokwanira bwino ya moyo, yomwe imawaphunzitsa asilamu kuti akhale apakatikati, ndi achikhalidwe chabwino, ndi otenga nawo gawo mdera. Nkhani ya kupembedza m'chisilamu, simangokhudza kupemphera kasanu kokha, kapena kupempha pempho kwa Mulungu ayi, koma ndi chinthu chachikulu chomwe chikukhudza ntchito iliyonse yomwe imamusangalatsa Mulungu (Allah). Ndipo zitsanzo zina za zimenezi;

- Kupeza zofunikira za pamoyo mu njira yachilungamo
- Kuthetsa moyo wopondelezana
- Kuwasamalira ana amasiye
- Kusamalira chilengedwe
- Kupirira ndi kudzichepetsa
- Kupindulira anthu a mdera lako
- Kuwalemekeza makolo
- Kuima limodzi ndi chilungamo
- Kuwachitira zabwino oyandikana nawo nyumba
- Kumuopa Mulungu (Allah)
- Kusamalira banja
- Kuyankhula zowona


Ntchito za mapephero zimasaukira kukhala ndi chitsimikizo chowona chofuna kumusangalatsa Mulungu (Allah), ndipo zikuyenera kukwaniritsidwa molondola mogwirizana ndi ziphunzitso za chisilamu.

CONTENTS

































# CHISILAMU CHIMATI CHIANI PANKHANI YOKHUDZA AKAZI:

**Mkazi ali ndi ulemerero waukulu m'chisilamu.**

Akuyenera kuchitiiridwa chikondi, ndi kulemekezedwa, ndi kupatsidwa ulemu. Iwo ali ngati amuna pa kupatsidwa ufulu ndipo n'kosatheka kusintha mfundo imeneyi powapondereza kapena kuwakakamiza.

**Uchigawenga:**

Chisilamu chidaletsa kuwachita chiwembu anthu osalakwa, ndipo chadapanga zimenezi kukhala mulandu, popanda kuyang'ana zipembedzo zawo. Kupha, m'chipembedzo chachisilamu kudaloledwa pa zifukwa zotamandika monga kufuna kuteteza dera la anthu, ndi kuletsa kufalikira kwa kuponderezana ndi kupititsa patsogolo chilungamo.

**Chakudya chololezedwa:**

Zakudya zahalali ndi zimene chisilamu chimaziloleza kuzidya. Ndi chikakamizo kuzinga nyama ndi nkhuku mu njira yaumunthu komanso kuyesetsa kuchepetsa kuzunzika kwa nyamazo pamene zikuzingidwa, ndiponso ndi chikakamizo kutchula dzina la Mulungu (Allah) panthawi yozinga.

**Chikhulupiriro chakuti munthu wakhala akusintha kuchoka pa nkhwere kudzafika momwe alili lero:**

Mulungu (Allah) adamulenga munthu woyamba Adamu m'chilengedwe chake chokwanira monga munthu, osati kuti iye wakhala akusintha pang'onopang'ono kuchoka pa kukhala nkhwere wochangamuka mu zochita. Ndipo zimenezi (zakuti munthu woyamba adalengedwa yense wokwanira) n'zosatheka kuzitsimikizira kapena kuzikana mu njira yachindunji pogwiritsira ntchito sayansi chifukwa chakuti ndi chinthu chapaderadera (chosankhika) chomwe chidachitika mu hisitole (kutanthauza kuti ndi chozizwitsa), choncho sichingaunikidwe ndi ufufuzi wa sayansi.




HOTLINE
+971 56 204 2045
islamicicdxb
islamicic.com info@islamicic.com +971 4 355 5223
DOWNLOAD CHICHEWA FLYER
www.iicdxb.com/chichewa

CONTENTS


MAU OTSEGULIRA OFOTOKOZA CHISILAMU
MTUMIKI MUHAMMAD MTENDERE UKHALE PA IYE
YESU: MTHENGA WA MULUNGU (ALLAH)
MULUNGU M'CHISILAMU
KORANI
KODI CHOLINGA CHA MOYO NDI CHIANI?
KUCHIMVA MOLAKWIKA CHISILAMU
UFULU WA AKAZI M'CHISILAMU
KUSAKHULUPIRIRA MLENGI M'KAYANG'ANIDWE KA CHISILAMU
ZOZIZWITSA ZASAYANSI MU QUR'AN


# MTUMIKI MUHAMMAD

## MTENDERE UKHALE PA IYE

CHICHEWA (MALAWI) (02/11) النبي محمد عليه الصلاة والسلام FREE COPY

*Ukuyenera kumudziwa munthu ameneyu!*


Dar Al Ber Society
www.daralber.ae
الإمارات THE EMIRATES
Your Path To Peace..
مركز المعلومات الإسلامي
Islamic Information Center
للتعريف بالإسلام
تصريح رقم: (2017/139)
دائرة الشؤون الإسلامية والعمل الخيري
Islamic Affairs & Charitable Activities Department
www.islamicic.com

CONTENTS

































# MUHAMMAD MTENDERE UKHALE PA IYE NDI NDANI?

> *"Ndithu muli nacho chitsanzo chabwino mwa Mthenga wa Allah kwa yemwe akuopa Allah ndi tsiku lachimariziro, namatchula Allah kwambiri."*
> **Quran 33:21**

Asilamu amakhulupirira kuti Muhammad (mtendere ukhale ndi iye) ndi Mtumiki wotsiriza pa mndandanda wautali wa Atumiki amene adatumizidwa kudzawaitanira anthu kuti amugonjere ndi kumpembedza Mulungu Mmodzi Yekha (Allah pa chiarabu). Ena mwa Atumiki amenewa ndi: Adamu, Nowa, Abrahamu, Ishmaeli, Isaki, Davide, Solomoni ndi Yesu (mtendere ukhale pa Iwo onse).

Ngati momwe ziliri kuti Mose (mtendere ukhale ndi Iye) adatumizidwa ndi Buku la Torah (chomwe ndi chivumbulutso chenicheni chosasokonezedwa chomwe chidatumizidwa kwa Mose), komanso Yesu (mtendere ukhale pa iye) yemwe adatumizidwa ndi Buku la Chipangano chatsopano (chenicheni chomwe chidalipo pachiyambi, chosasokonezedwa, osati zolembedwa za lelozi), chimodzi-modzinso Asilamu amakhulupilira kuti Muhammad (mtendere ukhale pa iye) adatumizidwa ndi Korani kuti adzaonetse mmene ziphunzitso zake ziyenera kugwiritsidwira ntchito.

Mkazi wa Mtumiki Muhammad (mtendere ukhale pa iye) yemwe ndi 'A'isha, adafunsidwapo kuti afotokoze za chikhalidwe cha Mneneri Muhammad (mtendere ukhale pa iye), ndipo adayankha kuti iye adali 'Korani yoyenda', kutanthauza kuti adali kugwiritsira bwino zedi ziphunzitso zopambana za Korani pamoyo wake watsiku ndi tsiku. Tionetsa m'mene iye adazipangira ziphunzitso zapamwambazi kukhala ntchito zotamandika.

## NTCHITO YA MTUMIKI

> *"Ndipo sitidakutume koma kuti ukhale mtendere kwa zolengedwa zonse"*
> **Qur'an 21:107**

Kuwonjezera pa kuwaitanira anthu ku kupemphera, kusala chakudya ndi kupereka chopereka chaulere, Mtumiki (mtendere ukhale pa Iye) adaphunzitsanso kuti kukhulupirira mwa Mulungu (Allah) kukuyenera kumusintha munthu chikhalidwe chake cha momwe amawachitira anthu ena. Iye adati *"abwino mwa inu ndi amane ali ndi chikhalidwe chabwino."*

Zoyankhula zambiri za Mneneri (mtendere ukhale pa iye) zimatsindika kuti pali kulumikizana kwakulu pakati pa chikhulupiriro ndi ntchito, mwachitsanzo: *"Amene amakhulupirira Mulungu (Allah) ndi tsiku la chiweruzo, asapereke masautso kwa woyandikana naye nyumba; ndipo amene amakhulupirira Mulungu (Allah) ndi tsiku la chiweruzo ayenera kulandira mlendo wake*

CONTENTS




*mwaubwino; ndiponso amene akukhulupilira Mulungu (Allah) ndi tsiku la chiweruzo ayenera kulankhula zabwino kapena apo akhale chete.* Al Bukhary (6018)

Mthenga wotsiriza (mtendere ukhale pa iye) adawaphunzitsa anthu kuti azichitirana chisoni ndi kulemekezana wina ndi nzake: *"Amene sachitira chisoni ena, nayenso sadzachitiridwa chisoni"* Al Bukhary (5997)

Ndipo m'kufotokoza kwina, anthu ena adamupempha Mneneri (mtendere ukhale pa iye) kuti apemphe kwa Mulungu (Allah) kuti awalange anthu osakhulupirira, koma iye adayakha kuti: *"Sindidatumizidwe kudzatemberera (anthu), koma ndatumizidwa kuti ndikhale chisoni (kwa anthu)."* Muslim (2599)

*"Koma akhululuke ndi kuleka zimenezo. Kodi simufuna kuti Allah akukhululukireni? Allah ndi Wokhululuka kwambiri, Ngwachisoni chosatha (choncho nanunso teroni)"*
**Qur'an 24:22**

# KUKHULULUKA

Mneneri (mtendere ukhale pa iye) adali wokhululuka zedi komanso wachisoni zedi kuposa anthu onse. Wina akamuchitira zosayenera, iye amamukhulukira, ndipo pamene munthu akuonjezera kumuchitira nkhanza, iye amakhalanso wopirira zedi. Adali woleza zedi mtima ndi wokhululuka, makamaka pamene ali ndi mphamvu za kutha kubwezera.

Muhammad (mtendere ukhale pa iye) adali wokhululuka zedi, ndipo palibe mulandu uliwonse kapena nkhanza zilizonse zomuchitira iye zomwe iye samatha kuzikhululuka. Adali chitsanzo chabwino cha kukhululuka, ngati mmene zatchulidwira m'ndime yotsatirayi:

*"Gwiritsa kukhululuka (khala ndi khalidwe lokhululuka) ndipo lamula zabwino ndi kudzipatula ku (zochita zaumbuli)*
**Qur'an 7:199**

*"Ndithu wolemekezeka kwambiri mwa inu kwa Allah, ndi yemwe ali wowopa (zedi Allah)."*
**Qur'an 49:13**

# KUFANANA

Mu zoyankhula za Mtumiki (mtendere ukhale pa iye) zotsatirazi, iye adaphunzitsa kuti anthu onse ndi ofanana pamaso pa Allah:

*"Anthu onse adachokera mwa Adamu, ndipo Adamu adachokera ku dothi. Munthu wachiarabu sali wopambana kuposa yemwe sali wachiarabu, nayenso wakuda khungu sali wopambana kuposa woyera khungu; kupatula (kupambana) kudzera mu kumuopa Mulungu (Allah)."* Ahmad (23489)

*"Mulungu (Allah) sakuweruzani malingana ndi mawonekedwe anu kapena chuma chanu, koma amayang'ana mitima yanu ndi ntchito zanu"* Muslim (2564)

CONTENTS






Zikufotokozedwa kuti wophunzira wina wa Mneneri (mtendere ukhale pa iye) adamutchula moipa wophunzira wina ponena kuti, *"E, Iwe mwana wa mzimayi wakuda!"* Mneneri (mtendere ukhale pa iye) adakwiya ndipo adati *"Kodi ukumutoza iye chifukwa cha kuda kwa mayi wake? Ndithudi mwa iwe muli zotsarira za umbuli wa nthawi yakale Chisilamu chisanabwere."* Al Bukhary (30)

# KULOLERANA

*"Usabwezere choipa kwa amene akuchitira choipa, koma akhululukire ndi kwachitira zabwino."* Umu ndi m'mene Mtumiki womaliza wa Mulungu (Allah) (mtendere ukhale pa iye) ankayankhulira pa zoyambanayambana ndi zonyozananyozana za pakati pa anthu ake.

M'mabuku achisilamu muli nkhani zingapo zomwe Mneneri (mtendere ukhale pa iye) adali ndi mwayi wowabwezera amene adamulakwira, koma iye adapewa kutero.

*"Ndipo chabwino sichingafanane ndi choipa. Chotsani choipa (ngati chitakufikani kuchokera kwa m'dani), ndi (chinthu) chabwino; mapeto ake akhala kuti yemwe padali chidani pakati pako ndi pakati pake akhala ngati mthandizi wodalilika.*

Qur'an 41:34

Adawaphunzitsa anthu kuti azipirira pamene akumana ndi zovuto: *"Wamphamvu si amane amawagonjetsa anthu ndi nyonga zake, koma wamphamvu ndi amene amawugwira mtima wake pamene wakwiya"* Al Bukhary (6114)

Kupirira ndi kulolera sikutanthauza kuti Msilamu akhale wosakhudzika (wongololera zilizonse) kapena wosadziteteza yekha pamene wachitiridwa chiwembu. Mneneri Muhammad (mtendere ukhale pa iye) adayankhula kuti, *"Musalakelake kukumana ndi adani, koma mukakumana nawo adaniwo, khalani opirira (polimbana nawo)".* Al Bukhary (2966)

# KULEZA MTIMA

Wophunzira yemwe adagwira ntchito kwa Mtumiki Muhammad (mtendere ukhale pa iye) kwa zaka khumi, adati: *"Muhammad (mtendere ukhale pa iye) adali woleza mtima pochita naye iye: "Ndikachita china chake, sadandifunsepo kuti umachitiranji?; ndiponso ndikapanda kuchita chinthu, sadandifunsepo kuti "bwanji sudapange chakuti chakuti?"* Ahmed (12784)

Ulendo wina, mkazi wa Mtumiki (mtendere ukhale pa iye) adayankha mokwiya atanyozedwa ndi munthu wina.

Mneneri (mtendere ukhale pa iye) adamulangiza kuti: *"Khala wodekha*


*"Chifukwa cha chifundo chochokera kwa Allah, uli woleza mtima kwa iwo, (iwe Mtumiki Muhammad). Ndipo ukadakhala waukali wouma mtima, ndithudi akadakuthawa...."*

Qur'an 3:159

CONTENTS

























*ndipo upeze mtima E, Iwe 'Aisha, chifukwa Allah amakonda kuleza mu zinthu zonse."* Al Bukhary (6024)

Adanenanso kuti: *"Kudekha kukakhala pa chinthu chilichonse kumachikongoletsa chinthucho, ndipo kukachotsedwa mu chinthu chilichonse, kumachiipitsa chinthucho."* Muslim (2594)

# KUDZICHEPETSA

Mtumiki (mtendere ukhale pa iye) adali kuwaletsa anthu kuti asamailire chifukwa cha iye pofuna kumpatsa ulemu. Iye ankakhala pamene papezeka mpata pa gulu pa anthu, ndipo sankalakalaka malo wolemekezeka. Sadavalepo (chovala) chilichonse chomusiyanitsa ndi ophunzira ake kapena chomuonetsa kutukuka kwambiri kuposa iwo. Ankasakanikirana ndi osauka komanso ovutika. Ankakhala ndi anthu achikulire (okalamba) ndiponso ankawathandiza azimayi oferedwa amuna awo. Anthu osamudziwa amati akamuona samatha kumusiyanitsa ndi anthu ena pagulu la anthu.

*"Ndipo akapolo a (Allah) Wachifundo chambiri ndi omwe akuyenda padziko modzichepetsa, ndipo mbuli zikanena kwa iwo (mawu amwano) amaziyankha mawu abwino.*

Qur'an 25:63

Powayankhula ophunzira ake adati: *"Allah wavumbulutsa kwa ine kuti, khalani odzichepetsa. Aliyense wa inu asadzikweze kwa nzake, ndipo wina asapondereze nzake".* Muslim (2865)

Umo ndi momwe kudalili kudzichepetsa kwake, kotero kuti ankaopa kuti angapembedzedwe ndi kupatsidwa ulemelelo umene uli omuyenera Mulungu Yekha basi:

*"Musamapyole malire pa kunditamandira ngati m'mene amachitira Akhirisitu pomutamandira mopyola muyeso Yesu Mwana wa Mariya. Ine ndi kapolo wa Mulungu (Allah) basi; chomwecho ndiitaneni kuti Kapolo wa Allah ndi Mtumiki wake."* Al Bukhary (3445)

# MAMUNA WABWINO ZEDI

Mkazi wokondeka wa Mtumiki, Aisha, adafotokoza za mwamuna wake wolemekezeka (kuti): *"Iye nthawi zonse amathandiza ntchito za pakhomo, ndipo nthawi zina amasoka zovala zake, kukonza nsapato zake, ndipo ankagwira ntchito za pakhomo."* Ahmad (25341)

*"Ndipo khalani nawo (akazi anu) mwaubwino"*

Qur'an 4:19

Sikuti adali mwamuna wodzipereka chabe basi ayi, koma amawalimbikitsanso ophunzira ake kuti adzitsatira chitsanzo chake: *"Wokwanira zedi mwa okhulupira pa chikhulupiliro, ndi amene ali ndi chikhalidwe chabwino. Ndipo abwino zedi mwa iwo ndi amene ali abwino pa kukhala bwino ndi akazi awo."* Ahmad (24204)

CONTENTS






# CHITSANZO CHABWINO

> *"Ndipo ndithu uli nawo (iwe Muhammad) makhalidwe abwino".*
> Qur'an 68:4

Zomwe zatchulidwazi ndi gawo lochepa chabe la momwe Muhammad (mtendere ukhale pa iye) ankakhalira moyo wake. Zitsanzo za chifundo ndi chisoni zatchulidwazi, zingathe kukhala zododometsa (zodzidzimutsa) kwa anthu ena malingana ndi chithunzithunzi choipa cha Chisilamu chomwe chimaperekedwa ndi nyumba zofalitsa nkhani, komanso chifukwa cha kuchifotokoza molakwika chisilamu komwe kumachitika nthawi zonse.

N'zofunikira kwambiri kuti pamene munthu akuyesayesa kuchimvetsetsa Chisilamu, ayenera kupita mwachindunji komwe chisilamucho chimatengedwako: chomwe ndi Qur'an ndi zoyankhula za Mtumiki Muhammad (mtendere ukhale pa iye), ndi kuti wina aliyense asachiweruze Chisilamu pongotengera zolakwika za Asilamu ochepa.

# NDEMANGA ZOCHOKERA KWA OMWE SALI ASILAMU

Mahamta K Ghandi – yemwe ndi mkulu wa zandale ndi zauzimu mu zochitikachitika zomenyera ufulu m'dziko la India adati:

> ***"Udali moyo wosalimbana nazo zinthu, ndi kudzichepetsa kwake kotherathu kwa Mneneri (Muhammad mtendere ukhale pa iye), ndi kukhulupirika kwake polemekeza mapangano ake, ndi kudzipereka kwake kwakulu kwa anzake ndi ophunzira ake, ndi kulimba mtima kwake, ndi khama lake, ndi kusaopa kwake, ndi chikhulupiriro chake cholimba mwa Mulungu, komanso mu ntchito yake. Zimenezi – osati lupanga ayi, ndi zimene zidatenga zinthu zonse zomwe zidali patsogolo pawo ndi kuthana ndi chopinga chilichonse."***

George Bernard Shaw, Wolemba nkhani wa chiburitishi, adafotokoza kuti:

> ***"Dziko lapansi likusaukira munthu woganiza ngati Muhammad; anthu azipembedzo m'mibadwo yapakatikati, chifukwa cha umbuli wawo ndi kuganiza kwawo koperewera, adapereka chithunzithunzi cholakwika cha iye poti amamutenga kuti ndi mdani wa Chikhirisitu. Koma pambuyo poyang'ana nkhani ya munthu ameneyu ndaipeza kuti ndiyopereka chidwi komanso yododometsa zedi, ndipo ndikutsindika kuti iye sanali mdani wa Chikhiristu, koma m'malo mwake akuyenera kutchedwa kuti "mpulumutsi wa anthu onse." M'kuona kwanga, ngati akanapatsidwa mphamvu yoyendetsa dziko lero lino, akadatha kutikonzera mavuto athu ndi kukhazikitsa mtendere ndi chisangalalo chimene dzikoli likusaukira."***

HOTLINE
+971 56 204 2045
islamicicdxb
islamicic.com
info@islamicic.com
+971 4 355 5223
DOWNLOAD CHICHEWA FLYER
www.iicdxb.com/chichewa

CONTENTS


MAU OTSEGULIRA OFOTOKOZA CHISILAMU

MTUMIKI MUHAMMAD
MTENDERE UKHALE PA IYE

YESU: MTHENGA WA MULUNGU (ALLAH)

MULUNGU M'CHISILAMU

KORANI

KODI CHOLINGA CHA MOYO NDI CHIANI?

KUCHIMVA MOLAKWIKA CHISILAMU

UFULU WA AKAZI M'CHISILAMU

KUSAKHULUPIRIRA MLENGI
M'KAYANG'ANIDWE KA CHISILAMU

ZOZIZWITSA ZASAYANSI MU QUR'AN


# YESU:
## MTHENGA WA MULUNGU (ALLAH)

CHICHEWA (MALAWI) (03/11) النبي عيسى عليه الصلاة والسلام FREE COPY

***ASILAMU AMAMKONDA YESU (MTENDERE UKHALE PA IYE)***


جمعية دار البر
Dar Al Ber Society
www.daralber.ae

الإمارات
THE EMIRATES

Your Path To Peace..

مركز المعلومات الإسلامي
Islamic Information Center
للتعريف بالإسلام

تصريح رقم:
(2017/139)


دائرة الشؤون الإسلامية والعمل الخيري
Islamic Affairs & Charitable Activities Department

www.islamicic.com

CONTENTS

























Yesu ndi munthu wolemekezeka amene amakondedwa ndi kulemekezedwa ndi miyandamiyanda ya anthu padziko lonse, koma ngakhale zili choncho pali chisokonezo chachikulu pa zokhudza chikhalidwe chenicheni cha munthu wamkulu ameneyu. Asilamu ndi Akhirisitu onsewa amamulemekeza Yesu kwakulukulu, komabe amamuonanso Iye mosiyana.

Kabuku aka kali ndi cholinga chofotokoza bwino-bwino nkhani zokhudza Yesu: Kodi Yesu adali Mulungu? Kapena adatumizidwa ndi Mulungu? Kodi Yesu weni-weni yemwe amadziwika mu mbiri adali yani?

# YESU MONGA MULUNGU

Akhirisitu ena amanena kuti "Yesu ndi Mulungu", kapena kuti ndi mmodzi mwa milungu itatu. Kutanthauza kuti iye ndi chithunzithunzi kapena gawo la Mulungu padziko lapansi, ndi kuti Mulungu adatenga maonekedwe a munthu. Komabe malingana ndi Baibulo, Yesu anachita kubadwa, amadya, amagona amapemphera, ndipo kudziwa kwake kudali ndi malire. Mbiri zonsezi sizikumuyenera Mulungu. Mulungu ali ndi mbiri za chikwane-kwane, pamene munthu ndi wosiyana ndi zimenezo. Ndiye zingatheke bwanji kuti chimodzi chikhale zinthu ziwiri zotsutsana nthawi imodzi?

Chisilamu chimatiphunzitsa kuti Mulungu Ndiwokwanira nthawi zonse. Kukhulupirira kuti Mulungu adasandukapo munthu kuli ngati kunena kuti Mulungu ali kapena adakhalapo wosakwanira kanthawi kena. Mkhirisitu akuyenera kudzifunsa yekha kuti; kodi mfundo yakuti Mulungu amene nthawi ina yake adaali kamwana kosatha kudzithandiza kokha, amene samatha kukhala moyo popanda kudya, kumwa, kugona – Mulungu otereyu – angakhale Mulungu wake yekha-yekhayo Wamphamvu zosatha yemwe watchulidwa mchipangano chakale? Popanda kukaika, sangakhale Iyeyo.

Komabe, ena akhoza kufunsa kuti, "Ngati Mulungu amatha kuchita china chilichonse, kodi chomwe chingamukanikitse kusanduka munthu nchiani?

Malingana ndi tanthauzo lake, Mulungu sachita zinthu zotsutsana ndi Umulungu wake. Choncho ngati Mulungu atasanduka munthu ndi kutenga mbiri za umunthu ndiyekuti sangakhalenso Mulungu.

Ndime zina za Baibulo zofotokoza mwachidule zingathe kugwiritsidwa ntchito molakwika kuti zikutanthauza kuti Yesu – mnjira ina yake – ndi Mulungu. Koma tikayang'ana ndime zomveka bwino ndi zoyankhula mwachindunji, tikupeza kuti mobwereza-bwereza Yesu akutchulidwa kuti munthu wodabwitsa basi, palibenso china. M'Baibulo muli ndime zimene Yesu akuyankhula m'menemo, ndi kuchita machitidwe owonetsa kuti Iye ndi Mulungu ndi wopatukana (siamodzi ayi). Mwachitsanzo, Yesu "adagwa nkhope pansi napemphera" [Mateyu 26:39].


Ngati Yesu adali Mulungu, ndiye Mulungu angagwe bwanji nkhope pansi ndi kupemphera? Ndipo nanga Iyeyo amapemphera kwa ndani?

CONTENTS































Baibulo likumutchula Yesu kuti Mneneri [Mateyu 21:10-11], choncho kodi zidatheka bwani Yesu kukhala Mulungu ndikukhalanso Mneneri wa Mulungu nthawi yomweyo?

Yesu adati, 'Ine ndikupita kwa Atate, pakuti Atate ndi wamkulu kuposa Ine.' [Yohane 14:28].

Yesu adati, '...ndikwera kunka kwa Atate wanga, ndi Mulungu wanu [Yohane 20:17]. Ngati Yesu adali Mulungu, ndiye nchifukwa chiani akunena kuti, 'kwa Mulungu wanga, ndi Mulungu wanu,'. Ndiponso kodi iyeyo amakwera kupita kwa ndani?

Ngati Yesu adali Mulungu, akadawawuza anthu momveka bwino kuti amupembedze, ndipo akadapezekamo m'baibulo mavesi onenetsa za zimenezi; koma ayi ndithu, iye adachita zosemphana ndi zimenezi ndipo adamudzudzula aliyense wofuna kumupembedza Iye: "Ndipo akundipembedza pachabe..." [Mateyu 15:9].

# "MWANA WA MULUNGU?"

Akhirisitu ena ndiye amanena kuti Yesu ndi mwana wa Mulungu. Kodi zimenezi zimatanthauza chiani? Chifukwa popanda kukaika Mulungu ali kutali zedi ndi izi zokhala ndi mwana weni-weni wamamuna. Anthu amakhala ndi ana, amphaka amakhala ndi ana a mphaka. Tsono zimatanthauza chiani akamati Mulungu ali ndi mwana?

> ***"Nkosayenera kwa Allah (Mulungu Mmodzi Yekah) kudzipangira mwana. Iye (Mulungu) wapatukana ndi zimenezi. Akafuna chinthu amangonena kwa chinthucho "chitika" ndipo icho chimachitikadi"***
>
> **Quran 19:35**

Mmalo moligwiritsira ntchito mtanthauzo lake leni-leni, tikupeza kuti liwu lakuti "Mwana wa Mulungu" mziyankhulo zakale za mabaibulo, limagwiritsidwa ntchito pofuna kusonyeza "munthu wabwino", ndipo lidagwiritsidwapo ntchito kwa Davide, Solomoni ndi Israyeli – , osati kwa Yesu yekha ayi. "....Israyeli ndiye mwana wanga woyamba wamamuna." (Exodus 4:22). Yense woyera watchulidwa kuti "mwana" wa Mulungu. "Onse amene atsogoleledwa ndi mzimu wa Mulungu ali ana amuna ndi akazi a Mulungu". [Aroma 8:14]

# "ATATE NDI MULUNGU"

Chimodzi-modzinso, pamene liwu lakuti 'Atate' likugwiritsidwa ntchito kumbali ya Mulungu, silikuyenera kutengedwa mwapamwamba ayi. Koma, ndi njira imodzi yonenera kuti Mulungu ndi Mlengi, Wopereka zofunikira za pamoyo, komanso Mfumu ndi Bwana wa zinthu zonse.


Komanso, Yesu nthawi zina ankatchedwa kuti 'Mbuye' ndi ophunzira ake. Liwu limeneli limagwiritsidwa ntchito mziyankhulo zeni-zeni zoyamba za baibulo, kutanthauza Mulungu komanso kwa anthu a ulemelero wawukulu. Mwachitsanzo, mchipangano chatsopano cholembedwa mchigiriki, liwu lakui 'kyrios' limagwiritsidwa ntchito

CONTENTS
































kwa 'Mbuye' komanso potchula dzina la mwini munda wa mphesa [Mateyu 20:8], komanso bwana amene adamumenya kapolo wosamvera [Luka 20:42-47].

Mmalo ena a baibulo, Yesu amatchedwa kuti 'kapolo' wa Mulungu malingana ndi ophunzira ake: "Mulungu wa Atate athu, wamulemekeza kapolo wake Yesu.". [Machitidwe 3:13]. Izi zikuonetserathu poyera kuti pamene liwu lakuti 'Mbuye' likugwiritsidwa ntchito kwa Yesu, ndi dzina la ulemu chabe, osati umulungu ayi.

# YESU: MNENERI

Malingana ndi chipembedzo cha chiyuda, Yesu amakanidwa kuti Iye sali Mesiya. Izi zikutsutsana kotherathu ndi ku Chikhirisitu, komwe Iye amapembedzedwa ngati Mulungu amene, kapena mwana wa Mulungu. Chisilamu chimatenga njira yapakati-kati, ndipo chimamuvomereza Yesu kuti ndi Mneneri wa Mulungu komanso kuti Iye ndi Mesiya. Koma Asilamu samupembedza Iye, pakuti kupembedzedwa nkwa Mulungu Yekha basi, amene adamulenga Yesu ndi zonse zomwe zikupezeka mdziko.

***"Yesu adati, 'Ndithudi, Ine ndine kapolo wa Allah...***

**Quran 19:30**

# KUBADWA KOZIZWITSA

Malingana ndi Qur'an, Mngero Gabiriyeli adatumizidwa kwa Mariya, namwala woyera, mkawonekedwe ka munthu, kudzamuwuza Iye kuti akhala ndi mwana amene adzabadwa mozizwitsa popanda bambo.

***'Iye [Mngero Gabiriyeli] adati, 'Ndithu Ine ndine Mtumiki wa Mbuye wako, (ndadza) kuti ndikupatse mwana woyera'. Adati: "Ndingakhale bwanji ndi mwana pomwe sadandikhudze mwamuna (aliyense), ndipo Ine sindili (mkazi) wachiwerewere?". Mngelo adati: "Ndi momwemo", Mbuye wako akuti: "Zimenezi kwa Ine nzosavuta. Ndipo timchita kukhala chozizwitsa kwa anthu ndi mtendere wochokera kwa Ife. Ndipo ichi ndi chinthu chimene chidalamulidwa kale"***

**Quran 19:19-21**


Ena ndiye amati kubadwa kwake kozizwitsaku ndi chizindikiro chakuti Iye ndi Mulungu. Koma, Yesu sadali woyamba kubwera mdziko lino popanda bambo, pakuti asanabwere Iye, Mneneri Adamu (mtendere ukhale pa Iye) anapezeka popanda bambo ingakhalenso mayi. Mulungu akuti:

CONTENTS

































***'Ndithu fanizo la Yesu kwa Mulungu lili ngati fanizo la Adamu; adamulenga ndi dothi namuuza kuti: "Khala munthu", ndipo adakhaladi. (Ichi ndi) choona chochokera kwa Mbuye wako; choncho usakhale mwa okaikira."***

Quran 3:59-60

Choncho ngati Yesu akupembedzedwa chifukwa cha kubadwa popanda bambo, ndiye mopanda kukaika nayenso Adamu ali oyenerera zedi kupembedzedwa pakuti adapezeka popanda kholo lililonse (mayi kapena bambo).

# ZOZIZWITSA ZA YESU (MTENDERE UKHALE PA IYE)

Yesu padatengedwa pathupi pake popanda bambo, ndipo Iye adachita zozizwitsa zikulu-zikulu mwachilolezo cha Mulungu.

Adayankhula akadali mchikuta powaimira ndi kuwateteza mai wake kwa anthu amene adawasinjirira za chiwerewere. Qur'an ikufotokozanso kuti Yesu adadzutsa akufa, adachiza akhate ndi akhungu – zonsezi mwachilolezo cha Mulungu.

Kuchita kwa zozizwitsa kwa Yesu (mtendere ukha pa Iye) sikutanthauza kuti Iye adali china chake choposa kukhala kapolo wodzichepetsa wa Mulungu. Ndipo, Atumiki ambiri adachita zozizwitsa, monga Nowa, Mose ndi Muhammad (mtendere ukhale pa Iwo), ndipo zozizwitsa zimenezi zimachitika mwachilolezo cha Mulungu, ndi cholinga chakuti awonetsere poyera kuwona kwa Mtumikiyo.

# UTHENGA WA YESU

Atumiki a Chipangano chakale, monga Nowa, Abrahamu, ndi Yona, sadalalikirepo zoti Mulungu ndi mmodzi wa atatu, ndiponso sadakhulupirire zakuti Yesu ndiye mpulumutsi.

***"Ndipo pamene Yesu adadza ndi zisonyezo zowonekera poyera, adati: "...Ndithu Mulungu Ndiye Mbuye wanga ndi Mbuye wanunso; choncho mpembedzeni; imeneyi ndiyo njira yolunjika."***

Quran 43:63-64

Uthenga wawo unali wodziwika bwino: Mulungu ndi Mmodzi, ndipo Iye Yekha ndi amene akuyenera kupembedzedwa. Kodi zingakhale zomveka kuti Mulungu atumize Aneneri kwa mazana-mazana a zaka ndi uthenga umodzi-modzi, kenako nkungowusintha mwadzidzidzi, nkuyamba kunena kuti tsopano Iye ndi mmodzi wa atatu, ndipo kenako nkupatula kuti chipumulutso chagona mkukhulupirira kuti Yesu ndiye Mulungu?


Zoona nzakuti, Yesu adalalikira uthenga wokha-wokhawo womwe adalilikira aneneri onse mChipangano chakale. Pali ndime m'Baibulo imene imatsindika pa mfundo imeneyi. Munthu wina adabwera kwa Yesu namufunsa kuti, 'Kodi lamuro lalikulu zedi ndi liti?'.

CONTENTS

































Yesu adayankha kuti, 'Lamuro lalikulu la malamuro onse, Imva Israyeli, Ambuye Mulungu wathu, Ambuye ndi Mmodzi.' [Maliko 12:28-29]. Choncho lamuro lalikulu zedi komanso chikhulupiriro chofunikira zedi malingana ndi Yesu, nchakuti Mulungu ndi Mmodzi. Akadakhala kuti Yesu ndi Mulungu, akadanena kuti, 'Ine ndine Mulungu, ndipembedzeni.' Koma mmalo mwake Iye adangobwereza vesi yochokera mChipangano chakale, kutsimikizira kuti Mulungu ndi Mmodzi.

Izi zikugwirizana ndi udindo wa Yesu, ngati momwe Chisilamu chaphunzitsira, kuti Yesu adatumizidwa kwa ana a Israyeli kudzatsimikizira uthenga wa Atumiki akale – omwe ndi: kukhulupirira mwa Mulungu Mmodzi Woona.

Monga Mtumiki wolemekezeka ndi wogonjera Mulungu, Yesu adagonjera mwachifuniro chake ku lamuro la Mulungu. Choncho, Iye adali 'Msilamu' – liwu lomwe likuyimira aliyense amene akugonjera chifuniro ndi malamuro a Mulungu.

# YESU MCHISILAMU

Yesu adali meneneri wolemekezeka wotumizidwa ndi Mulungu kuti akaitanire ku kumpembedza Mulungu Mmodzi Yekha.

Zimenezi zili poyera-yera m'Baibulo ndiponso zatsimikiziridwa ndi Qur'an. Chikhulupiriro chachisilamu pankhani ya Yesu chimafotokoza kuti Yesu weni-weni adali ndani, uku chikukhazikika pa chikhulupiriro cheni-cheni cha Mulungu ndi ukulu wake, kupatulika ndi kukwanira kwake.

Tikukuitanirani kuti muyang'anitsitse ndi kufufuza bwino zokhudza Chisilamu. Sichipembedzo china chabe ayi, koma ndi uthenga wokha-wokhawo umene adalalikira Nowa, Abrahamu, Mose, Yesu ndi Muhammad – mtendere ukhale pa Iwo onse. Chisilamu chimatanthauza 'kumgonjera Mulungu', ndipo ndicho njira yachilengedwe ndi yokwanira ya moyo wa munthu, imene imamulimbikitsa munthu kuti apereke chidwi chokwanira pa ubale wake ndi Mulungu ndi zolengedwa zake. Chisilamu chimaphunzitsa kuti Mulungu Ndiwachilungamo chonse komanso Wachifundo chosatha, ndipo Iye sasawukira kuti adzipereke Yekha nsembe pofuna kukhululuka machimo, ndiponso palibe aliyense wa ife amene 'anabadwa mu utchimo'. Mulungu amamuweruza aliyense malingana ndi zochita zawo, ndipo aliyense ali ofunsidwa pa ntchito zawo.

Chisilamu chimatiphunzitsa kuwakonda ndi kuwalemekeza Aneneri onse a Mulungu, koma kuwakonda ndi kuwalemekeza sikutanthauza kuwapembedza ayi, chifukwa chakuti kupembedzedwa nkwa Mulungu Yekha basi. Kumuvomereza Yesu monga Mneneri wa Mulungu ndi kukhala Msilamu, sikutanthauza kusintha kapena kutaya ukhrisitu wako ayi. Koma zikutanthauza kubwereranso kachiwiri ku ziphunzitso zeni-zeni za Yesu.

CONTENTS

MAU OTSEGULIRA OFOTOKOZA CHISILAMU
MTUMIKI MUHAMMAD
YESU: MTHENGA WA MULUNGU (ALLAH)
MULUNGU M'CHISILAMU
KORANI
KODI CHOLINGA CHA MOYO NDI CHIANI?
KUCHIMVA MOLAKWIKA CHISILAMU
UFULU WA AKAZI M'CHISILAMU
KUSAKHULUPIRIRA MLENGI
ZOZIZWITSA ZASAYANSI MU QUR'AN

# MULUNGU M'CHISILAMU

CHICHEWA (MALAWI) (04/11) مفهوم الإله في الإسلام FREE COPY

*Palibe wamkulu kuposa Mlengi Wamphamvu zonse*

جمعية دار البر
Dar Al Ber Society
www.daralber.ae

الإمارات
THE EMIRATES

Your Path To Peace..

مركز المعلومات الإسلامي
Islamic Information Center
للتعريف بالإسلام

تصريح رقم:
(2017/139)

دائرة الشؤون الإسلامية والعمل الخيري
Islamic Affairs & Charitable Activities Department

www.islamicic.com

CONTENTS






# KODI KULI MULUNGU?

Pali maumboni ambiri omveka omwe akutsimikizira za kulondola kwa chikhulupiriro chakuti kuli Mulungu yemwe adalenga chilengedwechi, ndipo tipereka maumboni atatu motere:

## 1. Dongosolo la chilengedwe chonse

Tayerekezerani kuti mukuyenda pagombe lalitali, mwapeza wotchi mumchenga, pamenepo simungaganize kuti wotchiyi inapangidwa mwangozi kapena inapezeka mumchengamo mwachisawawa, ndi kuti magawo ake onse opangidwa mozama komanso olukanalukana anapangika okha kuchokera ku zinthu zokwiriridwa mu nthaka. Ndithu wotchi iyi iyenera kukhala ndi woipanga kukhala chinthu chopezeka, ndipo ngati wotchi iyi ili ndi cholinga chomwe idipangidwira, chomwe ndi kunena nthawi molongosoka bwino, ndiye kuti woipanga wakeyo ayenera kukhala wodziwa, ndi kuti zochitika zachilengedwe sizingakwanitse kuipanga wotchi yomwe imagwira ntchito ndi dongosolo lolondola ndi lachindunji.

Tikaiyang'ana pulaneti ya Dziko Lapansi, tipeza kuti dongosolo lake la orbital mozungulira Dzuwa lasanjidwa ndi lakonzedwa bwino mu nthawi yake yolongosoledwa bwino kwambiri, zomwe zawathandizira asayansi kudziwa nthawi yotuluka ndi kulowa kwa dzuŵa. Monga momwe wotchi imayenera kukhala ndi Woipanga wodziŵa zedi amene amaisanja nthaŵi yake molondola, momwemonso Dziko Lapansi liyenera kukhala ndi Wolipanga Wodziŵa amene amadziŵa bwino lomwe nthaŵi ya kulizungulira kwake dzuŵa.

Momwemonso, pamene tikuona ndondomeko ndi malamulo osanjidwa mwaluso mkati mwa matupi athu komanso m'madera a dziko lonse lapansi, kodi si zomveka kuti chilengedwechi chili ndi wochilinganiza? Ndipo kufotokoza kwabwino kwambiri kwa "wolinganiza" ameneyu sikungakhale konena kuti pali Mulungu Mmodzi amene ali Wokhoza kulenga ndi kulinganiza chilengedwechi?!

## 2. Chiyambi cha Chilengedwe

Sayansi yamakono imanena kuti chilengedwe chili ndi chiyambi. Izi zachokera pa zimene azitulukira posachedwapa kuti Dzikoli likufutukuka, ndipo titati tibwerere m'mbuyo kwambiri, tipeza kuti Dziko limasonkhana kukhala chinthu chimodzi, kusonyeza kuti lili ndi chiyambi. Pali zifukwa zitatu zofotokozera chiyambi cha chilengedwe. Zingathe kukhala kuti:

> *Kuzindikira ndi kufufuza kumene anthu ali nako, kumatiwuza kuti chinthu chimene chili ndi chiyambi sichimangochokera pachabe.*

1. Chilengedwe sichidachokere ku kanthu kalikonse;
2. Chilengedwe chinadzilenga chokha, kapena
3. Chilengedwe chinachita kulengedwa.

CONTENTS






Ponena za kulongosola kwachiŵiri, ndiye kulingalira kosavuta kumatiuza kuti chinachake sichingachite kalikonse chisanakhaleko. Izi zikusiya mfundo yachitatu kukhala malongosoledwe okhawo anzeru, omwe ndiakuti: Mulungu Wolenga Wakutha, Waluntha ndiamene adalenga ndi kuchilongosola bwino bwino chilengedwechi.

Anthu ena angafunse kuti, "Kodi ndani analenga Mulungu"? Mulungu, Wolenga, ali wosiyana ndi chilengedwe chake. Akadakhala wofanana ndi chilengedwe, akadafunanso mlengi, ndipo zimenezi zingathe kupangitsa kuti pakhale gulu mndandanda wa alengi wopanda malire, chomwe ndi chinthu chosatheka. Pakuti Mulungu (Allah) ali kunja kwa malire a nthawi ndi malo a chilengwedwechi. Iye wakhala alipo ndipo alibe chiyambi, choncho funso loti ndani adalenga Mulungu ndi lopanda nzeru.

## 3. Chivumbulutso chochokera kwa Mulungu

*Ngati Mulungu anavumbulutsa buku la chitsogozo kwa anthu, ndiye kuti buku loterolo likuyenera kukhala ndi umboni wotsimikizirika wakuti kuli Mulungu.*

Pali zisonyezo zoonekeratu kuti buku la Chisilamu, Quran, ndi mawu a Mulungu. Pansipa pali kufotokoza kwachidule zifukwa zomwe zikuthandizira mfundo imeneyi:

- Korani idavumbulutsidwa zaka 1400 zapitazo ndipo ili ndi mfundo zambiri za sayansi zomwe anthu a nthawiyo sankazidziwa zomwe zapezedwa posachedwapa ndi sayansi yamakono. Zitsanzo ndi izi: madzi kukhala gwero la zamoyo zonse (Quran 21:30); Dzikoli likufutukuka ( Qur'an 51:47 ); ndi njira za dzuwa ndi mwezi, chilichonse njira yake payokhapayokha (Quran 21:33).
- Qur'an ili ndi mbiri yodziwika bwino yomwe anthu a nthawiyo sankaidziwa, komanso maulosi ambiri omwe atsimikizika kuti ndi olondola.
- Qur'an ilibe cholakwa chilichonse kapena kutsutsana.
- Qur'an yasungidwa, liwu ndi liwu, kuchokera pamene idavumbulutsidwa m'chiyankhulo chake chenicheni cha Chiarabu, mosiyana ndi mabuku ena omwe sakupezeka m'chiyankhulo chenicheni choyambirira.
- Korani ili ndi uthenga wosavuta, wangwiro komanso wapadziko lonse umene umakopa zikhulupiriro za munthu zokhudza Mulungu (Allah) Wamphamvu zonse.
- Korani idavumbulutsidwa kwa Mtumiki Muhammad (madalitso ndi mtendere zikhale pa iye) yemwe adali wodziwika m'mbiri ya anthu kukhala wosatha kulemba ndi kuwerenga. Komabe, Korani ili ndi chilankhulo chapadera chomwe chimadziwika padziko lonse lapansi kuti ndi pachimake pa chilankhulo cha Chiarabu komanso kukongola kwa zinenero.


*Kufotokozera komveka bwino kwa zinthu zambiri zapadera ndi zozizwitsa za Korani ndikonena kuti idachokera kwa Mulungu (Allah).*

CONTENTS

































# KODI MULUNGU NDI NDANI?

"Allah" ndi dzina laumwinimwini la Mulungu Mmodzi Woona, ndipo alibe china chilichonse chingatchedwe ndi dzina limeneli loti "Allah." Dzina limeneli lilibe kuchuluka kapena jenda mosiyana ndi liwu lachingerezi lakuti "God (Mulungu pa Chichewa," lomwe limatheka kulitchula mochulukira "gods/milungu," komanso ngati chachikazi "goddess/mulungu wamkazi." Choncho kugwiritsiridwa ntchito kwapadera kwa dzina la "Allah" m'Chisilamu, ndi chimene chikusonyeza kutsindika kwa chipembedzochi pa mfundo ya kukhulupirira mwa Mulungu Mmodzi Yekha.

*"Ndipo mulungu wanu ndi Mulungu Mmodzi. Palibe wopembedzedwa mwachoonadi koma Iye."*
Quran 2:163

Kukongola kwakukulu kwa Chisilamu ndi kwakuti chimavomereza ungwiro wathunthu, ukulu ndi umodzi wa Mulungu (Allah) popanda kunyengerera. Izi zimaonekera mu ziphunzitso zoyera za Chisilamu zokhudza mbiri za Mulungu (Allah) ndi maina Ake.

## Mulungu ndi Mmodzi, Wosiyana ndi zonse:

- Mulungu (Allah) alibe nzake, alibe wofanana naye, alibenso mthandizi.
- Mulungu (Allah) alibe bambo, mayi, ana aamuna, aakazi kapena akazi.
- Mulungu (Allah) Yekha ndiye woyenera kupembedzedwa.
- Pakadakhala kuti pali milungu woposera m'modzi, zikanasonyeza kupereŵera kwa mphamvu zawo ndi ulamuliro wawo, chifukwa popanda kuchitira mwina, pakadakhala kutsutsana kapena kupikisana ndi milungu inayo.

## Mulungu (Allah) ndiye Wamphamvu zonse:

- Mulungu (Allah) ali ndi ulamuliro ndi mphamvu pa zinthu zonse.
- Chilichonse ndi chogonjera ndi chodalira pa Iye.
- Kumumvera Mulungu (Allah) sikuchulukitsa Mphamvu Zake, komanso kusamumvera sikuchepetsa mphamvu Yake mwanjira iliyonse.

## Mulungu ndiye Wapamwambamwamba;

- Palibe chilichonse chomwe chingakhale pamwamba pa Mulungu (Allah), ndiponso palibe chilichonse chofanana naye.
- Makhalidwe a Mulungu (Allah) safanana ndi chilengedwe Chake.
- Palibe gawo la Mulungu (Allah) lomwe limapezeka mwa wina aliyense kapena china chilichonse.
- Mulungu ndi wangwiro ndipo alibe malire a munthu, monga kupuma pa tsiku lachisanu ndi chiwiri kuchokera pamene adalenga chilengedwe chonse m'masiku asanu ndi limodzi, monga momwe zipembedzo zina zimanenera.


## Mulungu (Allah) ndiye Wolungama ndi Wachisoni:

- Mulungu (Allah) safunikira kudzipereka yekha nsembe kuti akhululuke machimo chifukwa chakuti palibe munthu amene amabadwa mu uchimo.
- Mulungu amaweruza aliyense malinga ndi zochita zake ndipo aliyense adzayankha pa zochita zake.
- Anthu amapeza chiyanjo cha Mulungu (Allah) Wamphamvu zonse kupyolera m'kumukhulupirira Iye ndi kugwira ntchito zabwino, osati chifukwa cha mtundu, kapena ulemerero womwe ali nawo pakati pa anthu, kapena chuma.

CONTENTS



























# CHIKHALIDWE CHENI-CHENI CHA YESU

> *Pamene tikuyesayesa kufuna kumvetsetsa za chikhulupiriro cha Mulungu (Allah) mchisilamu, n'kofunikira kukamba za chikhalidwe cha Yesu, malingana ndikuti pali zonenedwa zambiri zosokoneza komanso mabodza okhudza kakhalidwe ka m'mene iye aliri.*

Akhirisitu ambiri amakhulupirira kuti “Yesu ndiye Mlengi”, kapena iye ndi m'modzi mwa milungu itatu, ndi kuti iye ndi chithunzithunzi cha Mulungu pano padziko lapansi, ndi kuti iye ndi Mulungu m'maonekedwe a munthu.

Komabe ngakhale zili choncho, malingana ndi bukhu loyera (Baibulo), Yesu anachita kubadwa ndipo amadya, amamwa, amagona, amapemphera, ndiponso kudziwa kwake kudali ndi malire; mbiri zonsezi sizikumuyenera Mulungu (Allah). Pakuti Mulungu ali ndi mbiri za chikwanekwane, pamene munthu ndi wosiyana ndi zimenezo. Ndiye zingatheke bwanji kuti chinthu chimodzi chipezeke mu zinthu ziwiri zotsutsana nthawi imodzi? Izi sizikugwirizana ndi nzeru ngakhale pang'ono.

Komabe, ena akhoza kufunsa kuti, “Ngati Mulungu (Allah) ali wakutha kuchita china chilichonse, chomwe chingamuletse kusanduka munthu n'chiani?

Malingana ndi tanthauzo lake Mlengi, sachita zinthu zotsutsana ndi umulungu wake. Choncho ngati Mulungu (Allah) atasanduka munthu ndi kutenga mbiri za umunthu ndiye kuti sangakhalenso Mlengi.

Kuwonjezera apo, mu Baibulo muli ndime zimene Yesu akuyankhula ndi kuchita machitidwe owonetsa kuti Iye ndi kapolo wa Mulungu (Allah), ndi kuti Mulungu ali wopatukana ndi iye (kutanthauza kuti siamodzi ayi). Mwachitsanzo, m'Baibulo Yohane 8/40: “Koma mmene zililimu, inu mwatsimikiza kundipha ine, munthu amene ndinakuwuzani choonadi chimene ndinachimva kuchokera kwa Mulungu.”

Akhiristu ambiri amakhulupiriranso kuti “Yesu ndi mwana wa Mulungu.” Tikuyenera kudzifunsa tokha kuti, kodi zimenezi zikutanthauzanji kwenikweni?

N'zachidziwikire kuti Mulungu (Allah) ali kutali zedi ndi kukhala ndi mwana mwanjira ina iliyonse. M'malo mwake tikupeza kuti malingana ndi mayankhulidwe akale a mabaibulo, liwu loti “mwana wa Mulungu” limagwiritsidwa ntchito pofuna kutanthauza “anthu oyera.” M'ndime zambiri za Chipangano chakale liwuli lagwiritsidwa ntchito kwa anthu ambiri oyera mtima, monga Davide, Solomoni ndi Israyeli – , osati kwa Yesu yekha ayi.

Chimodzi mwa zitsanzo ndi mau onena kuti: “....Israyeli ndiye mwana wanga woyamba wamamuna.” (Ekisodo 04:22).

Chikhulupiriro chachisilamu pankhani yokhuza Yesu chimafotokoza kuti Yesu weniweni (madalitso ndi mtendere zikhale pa iye) adali ndani, uku chikukhazikika pa chikhulupiriro chenicheni cha Mulungu (Allah) ndi ukulu wake, kupatulika ndi kukwanira kwake. Yesu adali Mtumiki wolemekezeka wotumizidwa ndi Mulungu (Allah) kuti aitanire ku kumpembedza Mulungu (Allah) Yekha.

> *“Sikoyenereka kwa Mulungu (Allah) kudzipangira mwana, Iye (Allah) wapatukana ndi zimenezi”*
> Qur'an 19:35

CONTENTS































## Mulungu Yekha ndiye woyenera kumpembedza

***"Ndipo mpembedzeni Mulungu (Allah), ndipo musamphatikize ndi chilichonse." Qur'an 4:36***

Ziphunzitso za Chisilamu zazikidwa pa mfundo yakuti tiyenera kuzipereka ntchito zonse zamapemphero kwa Mulungu (Allah) Yekha Wamphamvu zonse, palibe chinthu china choyenera kupembedzedwa kupatula Iye. Kuyambira mafano, kapena manda, kapena dzuwa, mwezi, nyama, aneneri kapena anthu olungama. Ngakhalenso angelo, ma sheikh kapena anthu ophunzira chipembedzo. Zonsezi zinalengedwa ndiponso zili ndi malire, ndipo mwa izo muli kuperewera ndi kulephera, pomwe Mulungu (Allah) Yekha Wamphamvu zonse ndiamene ali ndi ungwiro wotheratu.

## Mulungu Wamphamvu zonse amapembedzedwa mwachindunji popanda mkhalapakati

Mulungu (Allah) Wamphamvu zonse sasaukira othandizana nawo kapena akhalapakati, pakuti njira ndiyotsekuka pakati pa Mulungu (Allah) ndi anthu onse, angathe kumpembedze Iye Yekha mwachindunji ngati momwe Iye walamulira. Iye amawamva onse amene akumutamanda ndi kumuitana, ndi kumpembedza ndi kukhala ndi chiyembekezo mwa Iye. Koma kumpembedza Mulungu (Allah) kupyolera mwa akhalapakati ndi aomboli (monga mafano, mizimu, ndi zina zotero), kumaononga mizati ya umodzi wa Mulungu (Allah) Mmodzi Yekha ndiponso kumaphwasula mfundo yakuti Mulungu (Allah) Yekha ndiye woyenera kupembedzedwa osati wina aliyense.

## Atumwi onse anaitanira ku kumpembedza Mulungu (Allah)

***"Ndipo ndithu, ku mtundu uliwonse tidatumiza Mtumiki (wonena kuti): "Pembedzani Mulungu (Allah), ndipo mupewe milungu yabodza." Qur'an 16:36.***

Asilamu amakhulupilira mwa aneneri onse amene anatumidwa ndi Mulungu (Allah) Wamphamvu zonse, monga Adamu, Nowa, Abrahamu, Mose, Yesu, ndi Muhammad, mtendere ndi madalitso zikhale pa iwo. Mulungu (Allah) adawatumiza onsewa ndi uthenga umodzi: "Pembedzani Mulungu (Allah), inu mulibe mulungu wina koma Iye."

## Cholinga cha moyo... n'chakuti timupembedze Mulungu (Allah)

Cholinga chachikulu cha kukhalapo kwathu m'moyo uno ndicho kulambira Mulungu (Allah), kuvomereza umodzi wa umulungu Wake ndi umbuye Wake, ndi kuti timpembedze Iye Yekha, ndi kufunafuna chiyanjo Chake. Choncho nkhani ya kupembedza - m'Chisilamu – siimangokhudza miyambo yamapemphero monga kupemphera kasanu, ndi kusala kudya ayi, koma imakhudzanso chilichonse chimene Mulungu (Allah) amakonda ndi kukondwera nacho, monga makhalidwe a anthu olungama, zochita za anthu omvera, kupirira kwa iwo amene amagwira ntchito zabwino, ndi kuchitira zabwino osauka ndi osowa.

Pomaliza, maziko a Chisilamu ndi "kukhulupilira umodzi wa Mulungu (Allah) Wamphamvu zonse, Mlengi ndi Mbuye wa chinthu chilichonse, yemwe ali ndi mbiri za ungwiro, ndi kuti Iye Yekha ndiye woyenera kupembedzedwa. M'menemu muli kupambana kwathu m'moyo uno ndi wa pambuyo pa imfa.

HOTLINE
+971 56 204 2045
islamicicdxb
islamicic.com
info@islamicic.com
+971 4 355 5223
DOWNLOAD CHICHEWA FLYER
www.iicdxb.com/chichewa

CONTENTS


- MAU OTSEGULIRA OFOTOKOZA CHISILAMU
- MTUMIKI MUHAMMAD MTENDERE UKHALE PA IYE
- YESU: MTHENGA WA MULUNGU (ALLAH)
- MULUNGU M'CHISILAMU
- KORANI
- KODI CHOLINGA CHA MOYO NDI CHIANI?
- KUCHIMVA MOLAKWIKA CHISILAMU
- UFULU WA AKAZI M'CHISILAMU
- KUSAKHULUPIRIRA MLENGI M'KAYANG'ANIDWE KA CHISILAMU
- ZOZIZWITSA ZASAYANSI MU QUR'AN


# KORANI

CHICHEWA (MALAWI) (05/11) القرآن FREE COPY

## *Chivumbulutso chomaliza kwa Anthu*




جمعية دار البر
Dar Al Ber Society
www.daralber.ae

الإمارات
THE EMIRATES

Your Path To Peace..

مركز المعلومات الإسلامي
Islamic Information Center
للتعريف بالإسلام

تصريح رقم:
(2017/139)

دائرة الشؤون الإسلامية والعمل الخيري
Islamic Affairs & Charitable Activities Department

www.islamicic.com

CONTENTS






# KODI KORANI NDICHIANI?

## Mau a Mulungu

Korani ndi mau eni-eni a Mulungu Mmodzi Yekha, Wamphamvu (pachiarabu Allah), womwe adavumbulusidwa kwa Mneneri Muhammad (mtendere ukhale pa iye), kupyolera mwa Mngelo Gabiriyeli.

*"Kuvumbulutsidwa kwa Buku ili kwachokera kwa Mulungu (Mmodzi Yekha), Mwini mphamvu zoposa, Mwini nzeru zakuya".*

Qur'an 39:1

## Chiwongoko kwa anthu

*"Korani ndi "..chiwongoko kwa anthu .... komanso zizindikiro zoonekera poyera za chiwongoko, ndikutinso ikhale cholekanitsa (pakati pa choonadi ndi bodza).*

Qur'an 2:185

Imapereka njira yowathandizira anthu kusiyanitsa pakati pa chowonadi ndi chabodza, yomwe popando iyo anthu angathe kusokera.

## Chivumbulutso Chomaliza

Korani ndi buku lomalizira kuvumbulutsidwa ndi Mulungu Wamphamvu zonse (Allah), lomwe likutsimikizira zoona zochepa zomwe zidatsalira mmabuku akale, komanso likudzatsutsa zopeka ndi zowonjezera zomwe zidalowelera mmabukuwo, zomwe zikupezeka lero lino mkulembedwanso kwina kwa mabukuwo.

*"E, Inu amene mwapatsidwa Buku! Zikhulupirireni zomwe tavumbulutsa zotsimikizira zomwe muli nazo (kale)..."*

Qur'an 4:47

## Kodi Korani idavumbutsidwa motani?

Korani idavumbulutsidwa kwa Muhammad (mtendere ukhale pa iye), ndipo ikanali mchiyankhulo chomwe idavumbulutsidwira – chiarabu mpaka lero. Koma kumasulira kwa matanthauza a Korani kukupezeka mziyankhulo zosiyana-siyana.


Korani sidatsitsidwe monga ngati buku lokwanira mkuvumbulutsidwa kumodzi. Koma kuti idavumbulutsidwa pang'ono-pang'ono kwa zaka 23.

Pachifukwa chimenechi nkofunikira kudziwa kuti kodi iyo imavumbulutsidwa mogwirizana ndi zifukwa ziti kapena zochitika zanji, ndi cholinga choti tiimvetsetse bwino Koraniyi, kupanda kutero, ziphunzitso zake zingathe kumvedwa molakwika.


CONTENTS


























# Ndingadziwe bwanji kuti Korani Njoch

## Kutetezedwa (Kwake)

Korani ndi buku lokhalo la chipembedzo lomwe lakhala likuzungulira pakati pa anthu kwanthawi yaitali, koma ngakhale zili choncho likanali ndendende chimodzi-modzi ngati momwe lidalili nthawi yomwe linkavumbulutsidwa. Palibe chilichonse chimene chidawonjezeredwa, kuchotsedwa kapena kusinthidwa m'menemo, chiivumbulutsireni zaka 1400 zapitazo.

> *"Ndithu, Ife ndife omwe tavumbulutsa Korani, ndipo ndithudi tiisunga"*
> Qur'an 15:09

Korani siidasungidwe pongoilemba basi, koma yasungidwanso mmitima mwa asilamu; amuna, ana ndi akazi omwe. Lero lino, miyanda-miyanda ya anthu idaloweza Korani kumayambiriro mpaka kumapeto.

## Zozizwitsa za Sayansi

> *"Posachedwapa tiwaonetsa (awa okanira), zisonyezo zathu kumbali (zonse) za dziko ndi mwa iwo eni, kufikira zionekere kwa iwo kuti chimene wadza nachochi nchoona"*
> Quran 41:53

Korani siimatsutsana ndi Sayansi ya makono, koma imagwirizana nayo. Mbali imodzi yofunikira zedi ndiyakuti, m'Korani muli ndime zimene zikufotokoza molondola zedi zododometsa za chilengedwe za mitundu yosiyana-siyana ya maphunziro a Sayansi, monga embryology (nthambi ya Sayansi yokamba za mwana pamene ali m'chiberekero cha make), meteorology (nkhani zofufuza zanyengo), astronomy (nthambi ya Sayansi yofufuza za zinthu za mmalenga-lenga monga nyenyezi mapulaneti ndi zina), geology (nthambi ya Sayansi yofufuza za zinthu za mkati mwa nthaka monga miyala ndi zina), ndi oceanography (nthambi ya Sayansi yofufuza za nyanga zikulu-zikulu). Akatswiri a Sayansi adaipeza Korani kuti ndiyolondola zedi pa kafotokozedwe kake (mu zinthu zimenezi), chikhalirecho idavumbulutsidwa mu senchale ya chisanu nchimodzi (zaka 1300 zapitazo).

Komanso nkhani njakuti, zambiri mwa zozizwitsa za Sayansi zomwe zatchulidwa m'Quranizi, ndi zoti zangotulukilidwa kumene, kupyolera mu kupita patsogolo kwa zida za tekinoloje ya makono. Talingalirani mfundo zotsatirazi;

- Korani imafotokoza mwatsatane-tsatane za kukula kwa munthu m'chiberekero cha mai ake. Nkhani zimenezi sizimadziwika ndi Sayansi kufikira zaka zangopitazi.
- Sayansi yamakono yangozindikira kumene kuti pali chotsekereza chimene chimapangitsa kuti madzi a nyanja ziwiri zoyandikana asalowane, ndipo iliyonse ili ndi katenthedwe ndi kaziziridwe kake, kakhuthalidwe kake ndi kakomedwe kake kamchere.


Zisonyezo za Mulungu zimenezi zidafokozedwa m'Quran zaka zoposa 1400 zapitazo.

CONTENTS


































# okera kwa Mulungu Mmodzi Yekha?

## Kusafanana kwake ndi zinthu zina

Chiivumbulutsireni, palibe munthu ngakhale ndi mmodzi yemwe amene adakwanitsa kubweretsa chaputala chimodzi chofanana ndi Korani mkakongoledwe kake, kapena kumveka bwino kwa matanthauzo ake, kukhadwa kwake, luntha lake, maulosi ake, ingakhalenso mbiri zake zokwanira bwino.

"Ndipo ngati muli ndi chikaiko m'zomwe tamvumbulutsira kapolo wathu (kuti sizinachokere kwa Ife, koma wangopeka) tabweretsani surah imodzi yolingana ndi Koraniyi (mkayankhulidwe kanzeru ndi kayalidwe ka malamulo ake). Ndipo itanani athandizi anu (kuti akuthandizeni) kupatula Mulungu; ngati inu mukunena zoona (kuti Korani njopekedwa". Qur'an 2:23

Anthu amene adamkana Muhammad (mtendere ukhale pa iye) adalephera kukwaniritsa tchalenji imeneyi, ngakhale kuti iwo adali akatswiri pa chiyankhulo cha Korani (chiarabu). Tchelenji imenei ikadali yosayankhidwa mpaka lero.

## Ilibe Kudzitsutsa yokha

Pamene anthu akulemba zolemba-zolemba zawo amalakwitsa, monga katchulidwe ka mawu, malamuro a chiyankhulo, mfundo zodzitsutsa zokha, mfundo zolakwika, kuchotsedwa kwa mau, ndi zina zotero.

> *"Ndipo ikadakhala kuti siikuchokera kwa Mulungu Mmodzi Yekha, ndithudi m'menemo akadapeza kusiyana kwabiri..."*
> Qur'an 4:82

Korani ilibe kudzitsutsa kulikonse ngakhale mpang'ono. Kaya ndi kumbali ya kafotokozedwe ka zasayansi ya kayendedwe ka madzi, kakulidwe kwa mwana m'chiberekero cha mai ake, nkhani za zinthu za mnthaka monga miyala ndi zina, chiyambi cha dziko; mfundo zotsimikizika za histole ndi zochitika-chitika, ingakhalenso maulosi.

## Mwina Muhammad adailemba Yekha?

> *"Ndipo nkosatheka Korani iyi kukhala yopekedwa, yosachokera kwa Mulungu Mmdozi Yekha (Allah)"*
> Qur'an 10:37

Mneneri Muhammad (mtendere ukhale pa iye) ankadziwika mu mbiri yake kuti adali wosatha kulemba ndi kuwerenga. Sadaphunzirepo mtundu uliwonse wa maphunziro wothandizira luso la kufotokoza za sayansi molondola, kapena kukongola kwa buku lolemekezekali. Mafotokozedwe wolondola a nkhani za anthu akale ndi zitukuko zawo, amene atchulidwa m'Korani, ndiwododometsa zedi kotero kuti nkosatheka iyo kulembedwa ndi munthu.

CONTENTS






# Nchifukwa chiani idavumbulutsidwa?

Kuti anthu akhuulupirire Mulungu Mmodzi Woona

*"Ndipo Mulungu wanu ndi Mulungu Mmodzi basi. Palibe wopembedzedwa mwachoonadi koma Iye. Ngwachifundo chambiri, Ngwachisoni chosatha". Qur'an 2:163*

Nkhani yofunikira zedi yomwe yatchulidwa mKorani ndi nkhani ya kukhulupirira mwa Mulungu Mmodzi, Woona. Mulungu akutiwuza kuti Iye alibe mthandizi, alibe mwana, alibe wafanana naye, ndi kuti palibe amene ali ndi ufulu wa kupembedzedwa koma Iye basi. Palibe chofaniziridwa ndi Iye, ndipo palibe chilichonse mu zolengedwa zake chomwe chimafanana naye. Korani imakananso zomusimba Mulungu ndi mbiri za umunthu kapena kumupatsa Iye malire.

# Kuti idzakane milungu yabodza

*"Ndipo mpembedzeni Mulungu Mmodzi Yekha, ndipo musamphatikize ndi chilichonse." Qur'an 4:36*

Chifukwa chakuti Mulungu Mmodzi Yekha ndi Yekhayo amene ali oyenera kupembedzedwa mwachoonadi, milungu ina yonse iyenera kukanidwa. Korani ikukananso mfundo ya kumumveka wina wake – kupatula Mulungu Mmodzi Yekha, mbiri ya umulungu.

# Kuti idzafotokoze nkhani za kale

Korani ili ndi nkhani za mbiri zokhala ndi maphunziro abwino mkati mwake, komanso nkhani zoona za Aneneri monga, Adamu, Nowa, Abrahamu, Yesu ndi Mose. Pa nkhani zimenezi Mulungu Mmodzi Yekha akufotokoza motere:

*"Ndithu, mnkhani zawo izi muli phunziro kwa eni nzeru...". Qur'an 12:111*

# Kudzatikumbutsa za tsiku la Chiweruzo

Koroni yolemekezayi imatikumbutsa kuti wina aliyense adzalawa imfa ndipo akafunsidwa pa ntchito zawo ndi zoyankhula zawo;

*"Ndipo tsiku la Qiyamah tidzaika masikero achilungamo, chonncho mzimu uliwonse sudzachitidwa chinyengo chilichonse". Qur'an 21:47*


# Kudzakwaniritsa Cholinga chenicheni cha Moyo

Mwapadera-dera, Korani imatiphunzitsa kuti cholinga cha moyo nchakuti timpembedze Mulungu Mmodzi Yekha basi, ndi kuti tikhale moyo wathu mogwirizana ndi njira imene Iye adaikhazikitsa. Ku Chisilamu, kupembedza kumaimira ntchito ndi zoyankhula zonse (zamseri kapena zowonekera), zimene Mulungu Mmodzi Yekha amakondwera ndi kusangalala nazo. Choncho, pa kungochita zimene Mulungu Mmodzi Yekha walamula, ndiye kuti Msilamu akumupembedza Mulungu Mmodzi Yekha, ndiponso akukwaniritsa cholinga cha moyo. Zinthu zili mmusizi ndi zina mwa zitsanzo za kupembedza:


CONTENTS



























Kupemphera:

*"E, Inu amene mwakhulupirira! Weramani ndi kugwetsa nkhope zanu pansi, ndipo mpembedzeni Mbuye wanu ndi kuchita zabwino kuti mupambane". Qur'an 22:77*

Kupereka chaulere

*"......komanso perekani zimene wakupatsani, (mukatero) zikhala zabwino kwa inu. Dzichitireni nokha zabwino; ndipo amene watchinjirizidwa ku umbombo wake, iwowo ndiwo opambana". Qur'an 64:16*

Kukhulupirika:

*"Ndipo musasakanize choona ndi chonama; ndi kubisa choona uku inu mukudziwa". Qur'an 2:42*

Kudzisunga:

*"Ndipo auze Asilamu achimuna kuti adzolitse maso awo, ndipo asunge umaliseche wawo....".*

*"Ndipo auze Asilamu achikazi kuti adzolitse maso awo, ndipo asunge umaliseche wawo.....". Qur'an 24:30-31*

Kukhala othokoza

*"Ndipo Mulungu Mmodzi Yekha adakutulutsani mmimba mwa amayi anu pomwe simudali kudziwa chilichonse; ndipo adakupatsani kumva, kuona ndi mitima kuti muthokoze." Qur'an 16:78*

Kuchita chilungamo:

*"E, Inu amene mwakhulupirira! Khalani omiiritsa chilungamo, opereka umboni chifukwa cha Mulungu Mmodzi Yekha; ngakhale kuti ubwere ndi masautso kwa inu, kapena kwa makolo anu, kapena kwa abale anu, ngakhale ali olemera kapena osauka (musayang'ane zimenezo)...." Qur'an 4:135*

Kukhala opirira:

*"Ndipo pirira! Ndithu, Mulungu Mmodzi Yekha sataya malipiro a ochita zabwino.". Qur'an 11:115*

Kuchita zabwino

*"Mulungu Mmodzi Yekha walonjeza omwe akhulupirira ndi kuchita zabwino kuti adzapeza chikhululuko ndi malipiro aakulu." Qur'an 5:9*

## Kumaliza

Mwachidule, Korani imawaphunzitsa anthu momwe angampembedzere Mulungu Mmodzi Yekha, ndipo potero adzakhala kuti akukwaniritsa cholinga cheni-cheni pa moyo, ndi kupata kupambana mmoyo uno ndi otsatira.

*"Ndithu, Ife takuvumbulutsira (Iwe Muhammad) Buku ili chifukwa cha anthu. Choncho amene waongokoa, zabwino nza iye mwini. Koma amene wakhota ndiye kuti akudzikhotetsa yekha (ndipo zoipa za kukhotako zidzakhala pa iye yekha)...."*

Quran 39:41.

CONTENTS


MAU OTSEGULIRA OFOTOKOZA CHISILAMU
MTUMIKI MUHAMMAD MTENDERE UKHALE PA IYE
YESU: MTHENGA WA MULUNGU (ALLAH)
MULUNGU M'CHISILAMU
KORANI
KODI CHOLINGA CHA MOYO NDI CHIANI?
KUCHIMVA MOLAKWIKA CHISILAMU
UFULU WA AKAZI M'CHISILAMU
KUSAKHULUPIRIRA MLENGI M'KAYANG'ANIDWE KA CHISILAMU
ZOZIZWITSA ZASAYANSI MU QUR'AN


# KODI CHOLINGA CHA MOYO NDI CHIANI?


CHICHEWA (MALAWI) (06/11) الغاية من الحياة FREE COPY


*Kodi ndidachokera kuti?*

*Nchifukwa chiani ndili pano?*


*Nanga ndikupita kuti?*


Dar Al Ber Society
www.daralber.ae
الإمارات
THE EMIRATES
Your Path To Peace..
مركز المعلومات الإسلامي
Islamic Information Center
للتعريف بالإسلام
www.islamicic.com
تصريح رقم:
(2017/139)
دائرة الشؤون الإسلامية والعمل الخيري
Islamic Affairs & Charitable Activities Department

CONTENTS

























# KODI CHOLINGA CHA MOYO NDI CHIANI?

***Limodzi mwa mafunso amene amabwera mmaganizo pamene tikulingalira za cholinga cha moyo wathu ndiloti "tidachokera kuti?"***

Kodi tinangopezeka pano mwangozi chabe, kapena pali cholinga cha wina wake amene ali ndi nzeru za pamwamba, wolenga? Kuvomereza za kupezeka kwa wolenga ndi chiyambi cha kumvetsetsa cholinga chathu chenicheni pa moyo. Zifukwa zongogwiritsira ntchito nzeru chabe zilipo zambiri zimene tingagwiritsire ntchito pofuna kumkhulupilira Mlengi. Zifukwa zitatu zatchulidwa pansipa:

## 1. Chiyambi cha Dziko

Umboni woyamba womwe ukusonyeza kuti kuli Mlengi, ukukhudzana ndi kumvetsetsa bwino za chiyambi cha dzikoli.

***Tangoyerekeza kuti uli mkati moyenda ku chipululu nkuipeza wotchi. Tonse tikudziwa kuti wotchi imawumbidwa ndi galasi, pulasitiki ndi chitsulo. Galasi limachokera ku mchenga, pomwe pulasitiki amachokera ku mafuta, ndipo chitsulo chimachokera ku nthaka; zinthu zonsezi zimapezeka ku chipululu. Kodi iweyo ungakhulupirire kuti wotchiyi idadzipanga yokha? Kuti dzuwa lidawala, mphepo nkuwomba, mphenzi nkumenya, mafuta nkukhovokera pamwamba pa nthaka, nkusanganikirana ndi mchenga ndi chitsulo chija, ndipo kenako patapita zaka miyanda-miyanda wotchi nkuwumbika yokha mwachilengedwe?***

Malingana ndi Sayansi yamakono, ikutiwuza kuti dziko lili ndi chiyambi. Kodi dzikoli lidachokera kuti? Malingana ndi chizolowezi ndi nzeru za munthu wina aliyense (popanda kulimbira kukhala ndi maphunziro ambiri), timadziwa kuti chilichonse chimene chili ndi chiyambi sichingangoyamba chokha-chokha popanda wochiyambitsa, ndipo sichingadzilenge chokha. Choncho mfundo yomveka ndi yotsimikizika ndiyakuti pali wina wake yemwe adalenga dzikoli. Mlengi ameneyu akuyenera kukhala Wamphamvu ndi Waluntha kotero kuti adakwanitsa kuchibweretsa chidziko chonsechi kukhala chinthu chopezeka, nalenga malamuro a zachilengedwe (Sayansi) omwe akuyendetsa dzikoli. Mlengi ameneyu akuyeneranso kukhala wosasawukira nthawi ndi malo, pakuti zonsezi zidayamba pamene dziko lidalengedwa. mfundo zonsezi zikumanga phata la chikhulupiriro chakuti kuli Mlengi.

> 'Kapena adalengedwa popanda Mlengi kapena iwo adadzilenga okha?'.
> Quran 52:35-6

Ena angathe kufunsa kuti: 'Kodi ndani amene adamulenga Mlengiyo?'

Allah yemwe ndi Mlengi, Ndiwosafanana ndi zolengedwa zake. Allah Ndiwamuyaya, adalipo nthawi zonse ndipo kupezeka kwake kulibe mathero. Choncho kufunsa kuti 'adamulenga Allah ndi ndani', limeneli ndi funso lopanda nzeru.

## 2. Kukwanira bwino kwa Dziko


Tsono ukhala umboni wachiwiri wosonyeza kuti Mlengi alipodi, ndiye ndi ndondomeko ndi kulingana bwino kwa chidziko chododometsa mkakhalidwechi.

CONTENTS






























Zingatheke chidziko chachikulu chododometsa ngati ichi kudzilenga chokha, popanda uyang'aniri ndi utsogoleri wa wina wake wamphamvu ndi waluntha lopanda malire?

Magawo ambiri mchidziko chimenechi amaonetserathu poyera kuti chidakonzedwa ndicholinga chothandizira moyo. Zinthu monga ngati kutalikirana kwa dziko lathuli ndi dzuwa, kukula kwa mphipi ya nthaka, mulingo wa liwilo lomwe dziko lathuli limathamangira pozungulira; mulingo wa mpweya wopumira mu mlenga-lenga (oxygen); ingakhalenso kapendekedwe ka dzikoli ndi zina. Kapimidwe ka milingo imeneyi kakadati kasiyane pang'ono chabe ndi momwe kalili panopa, mowo padziko pano sukadapezeka.

Choncho ngati momwe zilili kuti wotchi ili ndi amene adaikonza kuti idzisunga nthawi bwino-bwino, chimodzi-modzinso dzikoli lili ndi Nkozi wake Wanzeru kuti lidziyenda bwino-bwino mnjira yake popanda kuphonya. Kodi nzotheka zimenezi kuchitika mwa izo zokha?

Pamene tikuona ndondomeko zokhazikika mwa ife eni komanso padziko lonse, kodi sizingakhale zanzeru kunena kuti zili ndi amene adazikonza? Ndipo kumufotokoza kwabwino zedi Nkonzi ameneyu ndiko kukhulupirira kuti Allah alipo, amene adabweretsa ndondomeko zimenezi.

Nkoyenera kudziwa kuti Chisilamu chimalimbikitsa ufufuzi wa Sayansi ndi kulingalira. Ntchito ya Sayansi ndiyakuti imatatinthandizira kufotokozera bwino mitundu yosiyana-siyana imene Allah amaika mu zolengedwa zake, ndikutinso tiyamikire ndi kuzindikira bwino kukula kwa mphamvu ndi luntha lake. Kupita patsogolo pa mauzindikiri a zasayansi, monga ngati zidango-dango kapena zochitika zodabwitsa zomwe zimachitika mdzikoli; monga ndondomeko ya kayendedwe ka madzi (water cycle) ndi zina zangati zimenezi, zimapereka zisonyezo zakuti pali Mlengi ndi Nkonzi, osati kuti tipezerepo mtsutso wakuti Nlengi kulibe ayi.

## 3. Chivumbulutso kuchokera kwa Allah

Umboni wachitatu, ndi chivumbulutso chomwe Allah adapereka kwa anthu ngati chisonyezo chakuti Iye alipodi.

Chimodzi mwa zolinga zikulu-zikulu za buku la Chisilamu (Qur'an), ndicho kuwaitanira anthu kuti alingalire ndi kuyamikira za chilengedwe cha Allah, ngati njira imodzi ya kumukhulupirira. M'Qur'an yonse, Allah akuitanira kuti tipereke chidwi chathu ku kakonzedwe ndi kawumbidwe kake kododometsa ndi kochititsa kasu mdzikoli, zomwe zikukwanira kutiwonetsa kuti ndife zipatso za kukonza kwake, zolinga zake ndi luntha lake. Mwachitsanzo, Allah akunena kuti:

> *"Ndithudi, mchilengedwe cha thambo ndi nthaka, ndi kusinthana-sinthana kwa usiku ndi usana, ndi zombo zikulu-zikulu zomwe zikuyenda panyanja (zitasenza zinthu) zothandiza anthu, ndi madzi amene Allah wawatsitsa kuchokera kumitambo, naukitsira nawo nthaka pambuyo pokhala yowuma, nawanditsa m'menemo mtundu uliwonse wa nyama (chifukwa cha madziwo), ndi mkusinthana-sinthana kwa mphepo, ndi mitambo yomwe yalamulidwa kuyenda pakati pa thambo ndi nthaka; ndithudi, (mzimenezo) muli zisonyezo kwa anthu anzeru (kuti Allah alipo). "*


Kuwonjezera apo, pali zizindikiro zowonekera poyera zosonyeza kuti Qur'an ndi mawu a Allah.

*Kuwonjezera apo, pali zizindikiro zowonekera poyera zosonyeza kuti Qur'an ndi mawu a Allah.*

CONTENTS



























Qur'an:

- Ndiyotetezeka ku zolakwika kapena zotsutsana zilizonse.
- Idasungidwa lemba ndi lemba mchiyankhulo chake cheni-cheni chachiarabu kuchokera nthawi ya kuvumbulutsidwa kwake, kusiyana ndi mabuku ena.
- Qur'an idalowezedwa ndi asilamu miyanda-miyanda, yonse kumayambiriro mpaka kumapeto.
- Ili ndi uthenga wosavuta, woyera ndi woyenera anthu a mitundu yonse omwe umaziitanira nzeru za munthu ndi chikhulupiriro chake chachibadwa pa za chikhulupiriro mwa Allah.
- Ladutsa zaka zoposa 1400 lili ndi mfundo zambiri-mbiri zotsimikizika zasayansi, zomwe sizinkadziwika kwa wanthu a nthawi zimenezo, ndipo zangotulukilidwa posachedwapa ndi Akatswiri a Sayansi. Zina mwazitsanzo ndi izi: 'Madzi ndi tsinde la chiyambi cha moyo wa zinthu zonse (Qur'an21:30); 'Dzikoli likutambasuka ndi kukula' (Qur'an51:47); ndi 'Kuyenda mozungulira kwa dzuwa ndi mwezi' (Qur'an 21:33).
- Lili ndi mfundo zotsimikizika za histole (mbiri) zomwe sizinkadziwika kwa anthu a nthawiyo, komanso lili ndi maulosi ankhani-nkhani omwe atsimikizika kuti ndi owonadi.
- Qur'an ili ndi mphamvu yakuya ndi yaikulu pa (kusintha) miyoyo ya wanthu.
- Idavumbulitsidwa kwa Mneneri Muhammad (mtendere ukhale pa Iye) yemwe amadziwika kuti ndi wosadziwa kulemba ndi kuwerenga, chikhalirecho lili ndi chiyankhilo chozama mwapadera-dera, kotero kuti imadziwika padziko lonse kuti ndi tsinde la chiarabu chomveka bwino ndi chiyankhulo chokongola.
- Kafotokozedwe kogwirizana zedi ndi nzeru ka zodabwitsa ndi zozizwitsa zankhani-nkhani za Qur'an, nkakuti bukuli likuyenera kuchokera kwa Allah basi, palibenso china.

# Allah Amapereka Chiwongoko

Kutha kwa kuvomereza kuti tidalengedwa ndi Allah Wanzeru zoposa, tikuyenera kuyembekezera kuti atidziwitse cholinga chathu. Tingadziwe bwanji chimene Allah akuyembekezera kwa ife? Kodi tipitirize kukhala moyo omangoyesa-yesa, kapena tidzipangire tokha cholinga chathu? Kapena tidzingoyenda ndi mweza, kumangotsatira ena? Ayi. Allah adatumiza atumiki ndi chivumbulutso pofuna kutidziwitsa cholinga chathu.

Allah adatumiza mazana-mazana a Atumiki (amatumiza) osachepera mmodzi ku Ntundu uliwonse ndi uthenga ofanana: kupempedza Allah yekha ndi kutsatira chiongoko chake. Mugulumo (la Atumiki) muli Adam, Nowa, Abraham, Mose, Yesu ndi Muhammad (mtendere ukhale pa Iwo onse)

*Yesu ngati mmene adalili atumiki ena onse nayenso amachita zozizwitsa, ndipo amaitanira kwa Allah Mmodzi Oona.*
**Quran 19:36**

Mtumiki Muhammad (mtendere ukhale pa Iye) – yemwe ndi wotsiriza mu mndandanda wa Atumiki – adali chitsanzo chabwino kumbali ya kunena zoona, chilungamo, chikondi ndi kulimba mtima. Iye adatumizidwa ndi chivumbulutso chotsiriza chochokera kwa Allah, yomwe ndi Qur'an; kuti idzaonetsere poyera mmene ziphunzitso zake ziyenera kugwiritsidwa ntchito.

CONTENTS

































Quran ndi buku la chiwongoko likufotokoza mfundo zochuluka monga; cholinga cha kupezeka kwathu (pano padziko); Allah ndi ndani; ntchito zokondedwa ndi Allah ndi ntchito zosakondedwa ndi Allah; nkhani za atumiki ndi maphunziro omwe ali m'menemo; nkhani za munda wamtendere, za kumoto, ndi tsiku lachiweruzo. Ili ndi cholinga chofuna kuchotsa kamvetsetsedwe kolakwika kokhudza chikhalidwe cha Allah, monga ngati kufotokoza bwino mmene Yesu alili ndi udindo wake, poyerekeza ndi mmene alili Allah.

*Pamene tikuyesa-yesa kufuna kumvetsetsa za chikhulupilro cha Allah mchisilamu, nkofunikira kukamba za chikhalidwe cha Yesu, malingana ndikuti pali zonenedwa zambiri zosokoneza komanso mabodza okhudza kakhalidwe ka mmene iye aliri.*

## Chikhalidwe cheni-cheni cha Yesu

Akhirisitu ena amanena kuti "Yesu ndi Mlengi", kapena kuti ndi mmodzi mwa Milungu itatu. Kutanthauza kuti iye ndi chithunzi-thunzi ndi mbali imodzi ya Mlengi padziko lapansi, ndi kuti Allah adatenga maonekedwe a munthu. Komabe malingana ndi Baibulo, Yesu anachita kubadwa, amadya, amagona amapemphera, ndipo kudziwa kwake kudali ndi malire. Mbiri zonsezi sizikumuyenera Allah. Allah ali ndi mbiri za chikwane-kwane, pamene munthu ndi wosiyana ndi zimenezo. Ndiye zingatheke bwanji kuti chimodzi chikhale zinthu ziwiri zotsutsana nthawi imodzi? Izi sizikugwirizana ndi nzeru ngakhale pang'ono.

Komabe, ena akhoza kufunsa kuti, "Ngati Allah Ndiwakutha kuchita china chilichonse, chomwe chingamukanikitse kusanduka munthu nchiani?

Malingana ndi tanthauzo lake Mlengi, sachita zinthu zotsutsana ndi Umulengi wake. Choncho ngati Allah atasanduka munthu ndi kutenga mbiri za umunthu ndiyekuti sangakhalenso Mlengi.

Kuwonjezera apo mu Baibulo muli ndime zimene Yesu akuyankhula ndi kuchita machitidwe owonetsa kuti Iye ndi Mlengi  ndi wopatukana (siamodzi ayi).

Mwachitsanzo, Yesu "adagwa nkhope pansi napemphera" [Mateyu 26:39].

Ngati Yesu adali Mulungu, ndiye Mulungu angagwe bwanji nkhope pansi ndi kupemphera? Ndipo nanga iyeyo amapembedza ndani?

Akhiristu ena amanena kuti "Yesu ndi mwana wa Mulungu."  Tikuyenera kudzifunsa tokha kuti, kodi zimenezi zikutanthauzanji? Nzachidziwikire kuti Allah ali kutali zedi ndi kukhala ndi mwana mwanjira ina iliyonse.

Mmalo mwake tikupeza kuti malingana ndi mayankhulidwe akale a mabaibulo, liwu loti "mwana wa Mulungu" limagwiritsidwa ntchito pofuna kutanthauza "munthu wabwino". Mu chipangano chonse chakale liwuli lagwiritsidwa ntchito kwa anthu ambiri ochita zabwino, monga; Davide, Solomoni ndi Israyeli – , osati kwa Yesu yekha ayi. "….Israyeli ndiye mwana wanga woyamba wamamuna." (Exodus 4:22), chimodzi mwa zitsanzo.

*"Sikoyenereka kwa Allah kudzipangira mwana, Iye Allah wapatukana ndi zimenezi"*
**Quran 19:35**

Chikhulupiriro chachisilamu pankhani yokhuza Yesu chimafotokoza kuti Yesu weni-

CONTENTS






weni adali ndani, uku chikukhazikika pa chikhulupiriro cheni-cheni cha Allah ndi ukulu wake, kupatulika ndi kukwanira kwake. Yesu adali Mtumiki wolemekezeka wotumizidwa ndi Allah kuti aitanire ku kumpembedza Allah Yekha.

## Ndiye...Nchifukuwa chiani ndili pano?

Aliyense akhoza kuvomereza kuti ziwalo zathu zapathupi monga maso, makutu, ubongo ndi mitima, (zonsezi) zili ndi cholinga. Kodi sizingakhale zomveka kunena kuti munthu nayenso watunthu ali ndi cholinga?

Allah, Wanzeru zonse, sadatilenge kuti tizingoyumba-yumba popanda cholinga chilichonse, kapena kuti tingokwaniritsa zilakolako zathu. Koma tili ndi cholinga chapamwamba, chomwe ndi; kuvomereza ndi kupembedza Mulugu Mmodzi Yekha, kuti tikhale pa chiongoko cha Mlengi wathu. Chiongoko chimenechi chimatipangitsa kuti tikhale opambana ndi kukhala ndi moyo wodalitsika kumbali zonse. Izi  zikukhudza ntchito zabwino za aliyense payekha-payekha monga; kupemphera, komanso ntchito zopindulira anthu a dera lonse, monga; kukhala abwino kwa oyandikana nawo nyumba, kuthandiza banja lako, chilungamo, ndi kusamalira nyama zosiyana-siyana.

Allah amatiletsa kupembedza china chilichonse (monga zosema, dzuwa, mwezi, anthu oyera pa chipembedzo, abusa, ngakhalenso atumiki). Iye Safuna othandizana naye kapena akhala pakati. Aliyense akhoza kumpembedza Allah mwachindunji (mopanda kudutsira mwa wina).

Allah amafotokoza kuti moyowu ndi mayeso, ndipo anthu amayesedwa munjira zosiyana-siyana. Tilibe mphamvu pa zomwe zimachitika kwa ife koma koma tikhoza kukhala nazo kumbali ya momwe tingazilandilire. Kupilira ku mavuto, ndi kuthokoza pa madailtso, ndi njira yodziyikira chifupi ndi Allah, ndikupeza Paradiso yosatha. Tikuchenjezedwanso za chilango choipa zedi kumoto ngati tisankha kusakhulupilira ndi kukana malamulo ake.

## Ndiye... ndipange chiani tsopano?

Kuyesa chikhulupiriro cha munthu chagona mkugwiritsira ntchito nzeru polingalira ndi kuzindikira  zizizndikiro za Allah, ndi kukhala mogwirizana ndi chiongoko cha Iye. Izi zimachitika pa kugonjera malamulo a Allah, zimene pachiarabu zimatanthauza kukhala "Msilamu".

Mulungu, Mmodzi ndi Wolenga Yekhayo – yemwe ndi 'Allah' pachiarabu – wachipanga chisilamu kukhala chotheka kuchifikira wina aliyense, posatengera mbiri yake, kochokera kapena mmene alili panthawi ino. Ndiye kuti aliyense akhoza kukhala msilamu pa kungokhulupilira ndi kuyankhula mau a chikhulupiriro otsatirawa:

"Ndikuchitira umboni kuti palibe Mulungu wina oyenera kupembedzedwa mwachoonadi koma Allah, ndipo ndikuchitiranso umboni kuti Muhammad ndi Mtumiki wa Allah."

Kodi siidafike nthawi yakuti ukwaniritse cholinga chako cha moyo, (chomwe ndi) kugonjera choonadi ndi kuvomereza za Mlengi wako?

CONTENTS


MAU OTSEGULIRA OFOTOKOZA CHISILAMU

MTUMIKI MUHAMMAD — MTENDERE UKHALE PA IYE

YESU: MTHENGA WA MULUNGU (ALLAH)

MULUNGU M'CHISILAMU

KORANI

KODI CHOLINGA CHA MOYO NDI CHIANI?

KUCHIMVA MOLAKWIKA CHISILAMU

UFULU WA AKAZI M'CHISILAMU

KUSAKHULUPIRIRA MLENGI — M'KAYANG'ANIDWE KA CHISILAMU

ZOZIZWITSA ZASAYANSI MU QUR'AN


# KUCHIMVA MOLAKWIKA CHISILAMU

CHICHEWA (MALAWI) (07/11) مفاهيم خاطئة حول الإسلام FREE COPY

Kodi nchiani chomwe umachidziwa bwino-bwino chokhudza Chisilamu?


جمعية دار البر
Dar Al Ber Society
www.daralber.ae

الإمارات
THE EMIRATES

Your Path To Peace..

مركز المعلومات الإسلامي
Islamic Information Center
للتعريف بالإسلام

تصريح رقم:
(2017/139)

دائرة الشؤون الإسلامية والعمل الخيري
Islamic Affairs & Charitable Activities Department

www.islamicic.com

CONTENTS






# MAU OYAMBA

Chisilamu ndi chimodzi mwa zipembedzo zazikulu zedi padziko, koma nthawi yomweyonso ndi chimodzi mwa zinthu zomvedwa molakwika. Mabodza komanso mamvedwe olakwika osiyana-siyana okhudza Chisilamu akhala akufalitsidwa pa zifukwa zambiri, monga; zandale, zachuma, mafalitsidwe a nkhani mokondera, tsankho ingakhalenso kuwaopa 'ena ake'.

## Cholakwika 1 – "Asilamu sawafunira ena zabwino ndiponso sachita nawo mwaubwino"

Anthu ena amanama kuti ziphunzitso zachisilamu sizigwirizana ndi zikhalidwe zapamwamba za 'kumaiko a kuzambwe (Amereka)'. Kuyankhula kumeneku sikukuonjezera chilichonse ku chilungamo.

Tikutero chifukwa chakuti asilamu amasunga zikhalidwe zapamwamba zodziwika ku dziko lonse, monga:

- Kukhulupirika ndi chilungamo
- Kukwaniritsa lonjezo
- Kulolera ufulu wa chipembedzo
- Kulemekeza makolo, achibale, oyandikana nawo nyumba, ndi anthu achikulire
- kupereka chaulere, kuthandiza, ndi kuwayang'anira amphawi ndi osowa
- Kuchita zabwino kwa oyandikana naye nyumba
- Kupewa bodza, chinyengo, kutukwana ndi miseche

*"Abwino zedi mwa inu ndi amene ali ndi makhalidwe abwino zedi." Adatero Mneneri Muhammad (mtendere ukhale pa Iye)*

*Ahmad (24204)*

Asilamu amalamulidwa kutenga nawo gawo mwaubwino mdera lawo, ndikuti akhale ndi chikhalidwe chapamwamba mu zochita zawo.

## Cholakwika 2 - "Asilamu amapembedza Mulungu wina Wotchedwa Allah"

Liwu lakuti 'Allah' ndi liwu lachiarabu chabe loimira Mulungu Wamphamvu – lomwe ndi liwu lachiarabu la tanthauzo lokwanira bwino, losonyeza Mulungu Mmodzi Yekha. 'Allah' ndi dzina lokha-lokhalo lomwe Akhirisitu ndi Ayuda oyankhula chiarabu amagwiritsira ntchito pamene akumutchula Mulungu.


*Asilamu amapembedza Mulungu wake yemwe uja amene adapembedzedwa ndi Aneneri Nowa, Abraham, Mose ndi Yesu.*

Komabe, ngakhale kuti Asilamu, Ayuda ndi Akhirisitu (onsewa) amakhulupirira mwa Mulungu Mmodzi (yemwe ndi Mlengi), chabe kuti kamvetsetsedwe kawo za Iye kamasiyana kotherathu. Mwachitsanzo, Asilamu amakanirathu mfundo yakuti Mulungu ali ndi athandizi kapena kuti ndi mmodzi mwa 'atatu', ndipo iwo amamusimba Mulungu kuti Iye yekha ndiye Wachikwane-kwane.

CONTENTS


























## Cholakwika 3 – "Chisilamu chimalimbikitsa uchifwamba"

Nthawi zambiri ofalitsa nkhani amapereka chithunzi-thunzi cha msilamu aliyense amene akuchita nkhondo kuti iye ndi wachifwamba, posayang'ana kuti msilamuyo akuchita nkhondoyo mwachilungamo kapena ayi, kapena kuti iye akuwapondereza ena kapena iyeyo akuponderezedwa.

Malingana ndi chisilamu, kuwapha anthu osalakwa omwe sakumenya nawo nkhondoyo panthawi ya nkhondo, ndi chinthu choipa zedi. Ndipo asilamu saloledwa kuwononga zomera ndi ziweto popanda chifukwa, akakhala anthu ndiye wosachita kunena. Komabe izi zili chonchi, nkofunika kusiyanitsa pakati pa uchifwamba, ndi kulimbana ndi utsamunda, pakuti ziwirizi nzosiyana kotherathu.

Qur'an yafotokoza mwamvemvemve kuwopsa ndi kuipitsitsa kwa kupha munthu wosalakwa, ndipo yalimbikitsa za kufunikira kwa moyo wa munthu

*"……amene wapha munthu popanda Iye (wophedwayo) kupha munthu, kapena popanda kuchita chisokonezo padziko, ali ngati wapha anthu onse. Ndipo amene wamuleka munthu ali ndi moyo, ali ngati waapatsa moyo anthu onse.."*

Quran 5:32

## Cholakwika 4 - "Chisilamu chimapondereza Akazi"

Mchisilamu, amuna ndi akazi amaonedwa mofanana pamaso pa Mulungu kumbali ya kulipidwa pa zabwino, ndi kukafunsidwa pa zoipa zomwe amachita. Chinthu chokhacho chomwe chimawasiyanitsa anthu pamaso pa Mulungu, ndi mulingo wa kumuwopa kwawo Mulungu.

*"Ndithu wolemekezeka zedi mwa inu kwa Mulungu ndi yemwe ali woopa"*

Quran 49:13

Ndime iyi ikutiwonetsa kuti ulemelero weni-weni subwera chifukwa chakuti munthu ndi wolemera kapena wosauka, wakuda kapena woyera khungu, wamamuna kapena wamkazi, koma ulemelero umabwera chifukwa cha ungwiro ndi kudzipereka pamaso pa Mulungu.

Akazi adapatsidwa ulemu ndi ulemelero waukulu, monga kudzipezera zofunikira pamoyo, kusankha mamuna omanga naye banja, kupitiriza maphunziro awo, ndi ufulu wa kuthetsa banja, komanso kulandira nawo chuma chosiyidwa ndi womwalira.

*Allah, Mlengi wa akazi ndi amuna, adapereka maudindo ndi ntchito zosiyana kwa aliyense, potengera kusiyana kwa chilengedwe chawo.*

Koma mwatsoka, alipo akazi ena achisilamu amene akuponderezedwa ndipo sapatsidwa maufulu awo. Koma limeneli si vuto la Chisilamucho ayi. Vuto nlakuti mmaiko ena, anthu amatsatira miyambo ndi zikhalidwe zina zomwe zili kunja kwa Chisilamu.

CONTENTS




## Cholakwika 5 – "Quran ndi buku lina chabe la Mbiri kapena Ndakatulo"

Qur'an ndi mau opatulika a Mulungu Wamphamvu zonse, lomwe lidavumbulutsidwa kwa Mneneri Muhammad (mtendere ukhale pa Iye), kupyolera mwa mngelo Gabriyeli. Iyo ndi chinthu chosiyanitsira pakati pa choona ndi chonama, ndipo mkati mwake muli chiwongoko cha anthu onse kuti achitsatire. Qur'an imafotokoza nkhani zosiyana-siyana za mibadwo ya anthu omwe adapita, komanso mbiri za aneneri, ndi cholinga chakuti titengeremo phunziro. Imatiphunzitsanso za ife eni ndi Mlengi wathu, komanso cholinga cha kupezeka kwathu pano padziko, chomwe nchakuti timukhulupirire ndi kumpembedza Mulungu Yekha basi.

*Ndipo njira yabwino zedi yozindikirira zomwe zili m'Qur'an, ndiyo kuiwerenga nokha basi.*

Mulungu sadalenge wanthu kuti adzingoyumba-yumba popanda cholinga chilichonse ayi. Ndipo kumuyesa munthu pa chikhulupiriro chake kwagona pakuti agwiritsire ntchito nzeru zake, chifuniro ndi mphamvu za kuganiza kwake polingalira ndi kuzizindikira zisonyezo za Mulungu, ndipo chisonyezo chachikulu zedi mwa izo ndicho Qur'an.

Qur'an ili ndi zozizwitsa zambiri mkati mwake, zomwe cholinga chake nchakuti tisakhale ndi chikaiko pa za kudalilika ndi kuwona kwake.

## Cholakwika 6 - "Hijab ndi chinthu Chopondereza"

Pofuna kukwaniritsa Hijab, akazi achisilamu akuyenera kuti adziphimbe mwa manyazi ndi zovala zawo, zomwe sizingawonetse mmene thupi lawo lilili, pamaso pa amuna amene alibe nawo chibale cha kubadwana. Komabe izo zili choncho, Hijab sinkhani ya kungodziphimba pamwamba chabe ayi, koma imayang'ananso za kuyankhula mau abwino, kukhala ndi manyazi, ndi chikhalidwe chaulemu.

Ngakhale kuti kuvala hijab kuli ndi mapindu ambiri-mbiri, koma chifukwa chachikulu chimene akazi achisilamu amavalira hijab nchakuti ndi lamuro la Allah (Mulungu Mmodzi yekha), ndipo Iye ndi amene amadziwa zomwe zili zabwino zedi kwa zolengedwa zake.


Hijab imampatsa mphamvu mkazi polimbikitsa kukongola kwa uzimu mumtima mwake, osati kungokongoletsa mawonekedwe a pamwamba pake chabe basi. Imawapatsa akazi ufulu wa kutenga nawo gawo pantchito za mdera, uku nthawi yomweyo akudzisungira ulemu ndi manyazi awo.

Hijab siisonyeza kupanikizidwa, kuponderezedwa, kapena kutsekedwa pakamwa ayi. Koma kuti ndi chitetezo ku zitozo, kuchitidwa zoipa komanso kusalidwa mopanda chilungamo. Choncho ulendo wina mukadzamuona mkazi wachisilamu atadziphimba, muzadziwe kuti akuphimba mawonekedwe a pamwamba pake, osati ubongo wake kapena nzeru zake ayi.

CONTENTS
























## Cholakwika 7 - "Asilamu onse ndi maArabu"

20% yokha ya Asilamu padziko lonse ndi maArabu, kutanthauza kuti 80% yatunthu ya Asilamu si maArabu ayi. Mwachitsanzo chabe, pali amwenye ndi ma Indonezya ambiri achisilamu kuposa maArabu.

Chisilamu chimaphunzitsa kuti munthu saali womupambana nzake chifukwa cha mtundu kapena khungu, ndipo chimadana kotherathu ndi khalidwe losankhana mitundu. Chisilamu chili ndi uthenga wadziko lonse kwa anthu onse – kutanthauza kuti, aliyense angathe kupeza mtendere ndi kupambana pa kukhulupirira ndi kumpembedza Mulungu Mmodzi Yekha Woona.

## Cholakwika 8 - "Jihad ndi uchifwamba"

Tsinde la Jihad lagona pa kulimbikira ndi kudzipereka nsembe chifukwa cha chipembedzo, koma munjira yokhayo imene ili yomusangalatsa Mulungu. Pachiyankhulo, Jihad imatanthauza 'kulimbikira', ndipo ingathe kutanthauza kulimbikira kwa munthu pa kuchita zabwino, kupereka chopereka chaulere, kapena kutenga nawo gawo pa nkhondo yachisilamu. Tanthauzo lodziwika zedi la Jihad ndi kumenya nkhondo, yomwe imaloledwa pofuna kusunga mtendere wa mdera, kuchotsa kuponderezedwa kuti kusafalikire, ndi kupititsa patsogolo chilungamo.

## Cholakwika 9 - "Asilamu amapembedza Muhammad kapena 'Mulungu-Mwezi"

Mamvedwe ena wolakwika wokhudza Chisilamu ngakuti Asilamu amapembedza Mneneri Muhammad (mtendere ukhale pa Iye). Izi sizowona, ndipo zingathe kutsutsidwa mosavuta pogwiritsira ntchito kuyankhula kwa Mneneriyu (mtendere ukhale pa Iye) konena kuti: "Musanditamandire Ine kopyola muyeso ngati momwe Akhirisitu adamutamandira kopyola muyeso Yesu mwana wa Mariya. Ine ndine kapolo wa Mulungu, choncho mudzinditcha kuti 'kapolo wa Mulungu ndi Mtumiki wake" Al Bukhariy (3445)

*Chisilamu chimaphunzitsa kuwalemekeza Aneneri ndi Atumiki onse – koma kuwalemekeza ndi kuwakonda iwo sikutanthauza kuti tiwapembedze monga milungu.*

Bodza linanso pankhani yomweyi ndilakuti Asilamu amapembedza 'Mulungu Mwezi', zomwenso nzabodza lamkunkhuniza. Kupembedza mwezi, kapenanso chilichonse kusiya Allah, nkoletsedwa kotherathu mchisilamu.

*Allah akuyankhula kuti: "Musalambire dzuwa ngakhale mwezi, koma lambirani Allah (Mulungu Mmodzi Yekha) amene adazilenga (zimenezi) ngati inu mumapembedza moona."*

Quran 41:37

Chisilamu chimavomereza kukwanira kwathunthu, ukulu komanso kupatulika kwa Mulungu popanda kulekerera mzimenezi. Iye ndi Woona, ndi Wachifundo chosatha. Kumpembedza Iye Yekha ndi mfundo yofunikira zedi pa chikhulupiriro cha Chisilamu, monga ikufotokozera Qur'an mmalo ambiri.

CONTENTS

























## Cholakwika 10 - “Chisilamu chimaloleza maukwati okakamiza”

Maukwati ochita kukonzerathu ndi zina mwa zizolowezi ndi miyambo yofalikira mmaiko ambiri otukuka. Maukwati okakamizawa amasinjiririrdwa ku Chisilamu, chikhalirecho chimenechi sichinthu chopezeka pakati pa Asilamu okha, koma izi zimachitika ndi zolinga zaupandu wofuna kuthana ndi chipembedzochi.

Mchisilamu, amuna ndi akazi omwe ali ndi ufulu wa kusankha kapena kukana ukwati (ngati sadasangalatsidwe). Mneneri Muhammad (mtendere ukhale pa Iye) adati:

“Mkazi amene adakwatiwapo (Thayyib) ali ndi ufulu (mphamvu) pa iye mwini kuposa womuyang'anira wake. Ndipo namwali (mtsikana wosakwatiwapo) nayeso afunsidwe maganizo ake, ndipo akakhala chete ndiye kuti wavomereza (kukwatiwa).” Muslim (1421)

## Cholakwika 11 - “Chisilamu chimakakamiza anthu kulowa Chisilamu”

Ngakhale kuti Asilamu ali ndi udindo wofikitsa uthenga wabwino wa Chisilamu kwa ena, komabe palibe amene angakakamizidwe kuchilandira Chisilamu. Munthu kuti achilandire Chisilamu, akuyenera kuti mwachifuniro chake akhulupirire ndi kugonjera Mulungu Mmodzi Yekha, choncho malingana ndi tanthauzo la Chisilamu, ndiyekuti munthu sangakakamize kapena kukakamizidwa kuchilandira chipembedzochi.

> *“Palibe kukakamiza munthu kulowa mchipembedzo; kulungama kwaonekera poyera kusiyana ndi kusalungama.”*
> **Quran 2:256**

Talingalirani izi:

- Dziko la Indonezya lili ndi chiwerengero cha Asilamu chochuluka zedi, chikhalirecho palibe nkhondo iliyonse yomwe Asilamu adachita kumeneko kuti anthu alandire Chisilamu.
- Pali ma Arabu 14 miliyoni achikhirisitu, omwe akukhala mkatikati mwa dziko la Arebiya kwa zaka zambiri-mbiri.
- Chisilamu ndi chipembedzo chomwe chikufalikira mofulumira zedi ku Amereka lero lino (kuposa zipembedzo zonse).
- Ngakhale kuti kuthana ndi mchitidwe woponderezana, komanso kulimbikitsa chilungamo ndi zifukwa zomveka zochitira Jihad pa Chisilamu, komabe kuwakakamiza anthu kuti alandire Chisilamu si chimodzi mwa zifukwa zochitira Jihad.
- Asilamu adalamulirapo dziko la Spain kwa zaka 800, koma monsemo sadakakamize aliyense kuti alowe mchisilamu.

## Kumaliza

Kuchiphunzira Chisilamu kupyolera munjira zosayenera komanso mopanda kufufuza bwino-bwino nkowopysa zedi, ndipo kumabweretsa kuchimva Chisilamu molakwika. Choncho musasokeretsedwe pomangolandira zinthu zolakwika ndi zonama zokhudza Chisilamu – chomwe ndi chipembedzo chimene akuchitsatira anthu miyanda-miyanda, omwe akupyola kota ya anthu onse a dziko lapansi.

Kodi chiwongoko cha anthu onsechi – uthenga wa Chisilamu - , sichikuyenera kuchilingalira ndi kuchiphunzira mozama ndi mosamala?

HOTLINE
+971 56 204 2045
islamicicdxb
islamicic.com info@islamicic.com +971 4 355 5223
DOWNLOAD CHICHEWA FLYER
www.iicdxb.com/chichewa

CONTENTS

MAU OTSEGULIRA OFOTOKOZA CHISILAMU
MTUMIKI MUHAMMAD MTENDERE UKHALE PA IYE
YESU: MTHENGA WA MULUNGU (ALLAH)
MULUNGU M'CHISILAMU
KORANI
KODI CHOLINGA CHA MOYO NDI CHIANI?
KUCHIMVA MOLAKWIKA CHISILAMU
UFULU WA AKAZI M'CHISILAMU
KUSAKHULUPIRIRA MLENGI M'KAYANG'ANIDWE KA CHISILAMU
ZOZIZWITSA ZASAYANSI MU QUR'AN

# UFULU WA AKAZI M'CHISILAMU

CHICHEWA (MALAWI) (08/11) حقوق المرأة في الإسلام FREE COPY

*Ndiolemekezedwa.*

*Opatsidwa ulemu.*

*Okondedwa.*

Dar Al Ber Society
www.daralber.ae
الإمارات THE EMIRATES
Your Path To Peace..
مركز المعلومات الإسلامي
Islamic Information Center
للتعريف بالإسلام
تصريح رقم: (2017/139)
دائرة الشؤون الإسلامية والعمل الخيري
Islamic Affairs & Charitable Activities Department
www.islamicic.com

CONTENTS






# KUTSEGULIRA

Akazi m'Chislamu amaganiziridwa kuti amachitidwa mwaukapolo, apansi komanso opondereezedwa. Koma ali chonchodi? Kodi Asilamu miyandamiyanda ndiopondereza, kapena mamvedwe olakwikawa amachita kupekedwa ndi mafalitsidwe okondera a nkhani?

> *"Nawonso akazi ali ndi zofunika kuchitridwa (ndi amuna awo) monga m'mene zilili kwa akaziwo kuchitira amuna awo."*
>
> Qur'an 2:228

Zaka zoposa 1400 zapitazo, Chisilamu chidawapatsa akazi ufulu umene akazi a maiko akuzambwe (Amereka) angoyamba kuwupeza posachedwapa. M'zaka za m'ma 1930, Mzimai wotchedwa Annie Besant, adayankhula kuti: "Ndim'zaka makumi awiri chabe zapitazi momwe Akhirisitu a ku Ingalande (England) adavomereza ndi kuzindikira za ufulu wa mkazi pa kukhala ndi katundu (chuma), chikhalirecho Chisilamu chidaloleza ufulu umenewu kuchokera kale. Kunena zoti Chisilamu chimalalikira kuti akazi alibe mizimu, kutero ndi kuchisinjirira." (Moyo ndi ziphunzitso za Muhammad, 1932).

Amuna ndi akazi, onsewa adachokera kwa munthu mmodzi – Mneneri Adamu (mtendere ukhale pa Iye). Chisilamu sichimalola kwa aliyense wa iwo koma chilungamo ndi kuchitiridwa mwaubwino basi.

# MALIPIRO OFANANA NDI KUFUNSIDWA MOFANANA

Amuna ndi akazi amampembedza Allah mofanana, kutanthauza kuti amapembedza Mulungu Mmodzi (Allah), ndiponso amagwira ntchito zamapephero zofanana, ndiponso amatsatira buku limodzi lopatulika, ndiponso mfundo za chikhulupiriro chawo n'zofanana. Allah (liwu la chiarabu loimira Mulungu Mmodzi Woona wa zolengedwa zonse), amaweruza anthu onse mwachilungamo komanso mofanana. M'ndime zambiri za Quran, Allah wayankhula motsindika kuti Iye adzachita nawo mwachilungamo amuna ndi akazi, ndi kuwalipira onse moyenera:

> *"Allah waalonjeza okhulupirira aamuna ndi okhulupirira aakazi minda yomwe pansi pake mitsinje ikuyenda, adzakhala m'menemo nthawi zonse. Ndiponso mokhala mwabwino m'minda ya nthawi zonse (yosatha).*
>
> Qur'an 9:72


> *"Ndithudi Ine sindidzasokoneza khama (la ntchito yabwino) kwa ochita khama mwa inu, kaya atakhala mwamuna kapena mkazi, (pakuti) ndinu amodzi."*
>
> Qur'an 3:195

Ndime zimenezi zikuwonetsa kuti malipiro amakhala molingana ndi ntchito za munthu osati chifukwa cha kukhala mamuna kapena mkazi. Kukhala mamuna kapena mkazi kulibe gawo lililonse la m'mene munthu angalipidwire ndi kuweruzidwira.

CONTENTS
























Tikafanizira Chisilamu ndi zipembedzo zina, tiona kuti (Chisilamu) chimapereka chilungamo ku mitundu iwiri yonse ya anthu (amuna ndi akazi). Mwachitsanzo, Chisilamu chimakana mfundo yakuti Hava ndi amene adalakitsa osati Adamu pakudya chipatso kuchokera mu mtengo woletsedwa. Malingana ndi Chisilamu, Adamu ndi Hava onse awiriwa adachita tchimo, ndipo onse adalapa, ndipo Mulungu (Allah) adawakhululukira.

## UFULU WOFANANA PA MAPHUNZIRO

Onse amuna ndi akazi akulimbikitsidwa mofanana kuti afunefune maphunziro. Mtumiki (mtendere ukhale pa Iye) adati: "Kufunafuna maphunziro ndi kokakamizidwa kwa Msilamu aliyense." Sahih AlJame'e (3913)

Komanso, akazi ophunzira kwambri adapezeka mu nthawi ya Mneneri (mtendere ukhale pa Iye). Ena adali ochokera kubanja kwake, ndipo ena adali ophunzira ake kapena ana awo aakazi. Wodziwika zedi mwa iwo adali Aisha, mkazi wa Mneneri (mtendere ukhale pa Iye), yemwe kudzera mwa Iye gawo limodzi m'magawo anai (kota) la malamulo a Chisilamu lidafikitsidwa (kwa anthu).

Akazi ena adali akatswiri akuluakulu odziwa malamulo achisilamu, kotero kuti mpaka amuna ena adatchuka ndi kudziwika chifukwa cha kuphunzira kuchokera kwa iwo.

## UFULU WOSANKHA WOKWATIRANA NAYE

Chisilamu chamlemekeza mkazi pomupatsa ufulu wa kusankha mamuna wokwatirana naye, ndi ufulu wopitiriza kuitanidwa ndi dzina la kubanja kwawo akakwatiwa. Kuphatikiza apo, anthu ambiri ali ndi maganizo akuti makolo (achisilamu) amawakakamiza ana awo achikazi kulowa m'banja. Uwu ndi mchitidwe wa miyambo chabe, ndipo ulibe gawo ku Chisilamu. Ndipo zenizeni n'zakuti ndizoletsedwa (kutero).

Mu nthawi ya Mneneri Muhammad (mtendere ukhale pa Iye), mkazi wina anabwera kwa Iye ndipo adati, "Bambo anga andikwatitsa ndi nsiweni wanga pofuna kukweza nyota yawo pamaso pa anthu, ndipo ine ndakakamizidwa m'zimenezi". Mneneri adawaitanitsa bambo a mtsikanayo, ndipo pamaso pawo adampatsa mtsikanayo ufulu wopitiriza banjalo kapena kulithetsa. Iye adayankha kuti, "E, Mtumiki wa Allah! Ndavomereza zimene bambo anga achita, koma ndimafuna kuwaonetsa akazi ena kuti sangakakamizidwe (ndi aliyense) kulowa m'banja.

## UFULU OFANANA KOMABE NDI ANTHU OSIYANA

Pamene amuna ndi akazi ali ndi ufulu ofanana monga mwa mfundo yaikulu, komabe ufulu wapaderadera ndi maudindo ena amene aperekedwa kwa iwo sali ofanana. Amuna ndi akazi ali ndi ufulu ndi maudindo osiyana, othandizirana ena kwa anzake.

Posatengera zosiyana za kunja ndi mkati mwa thupi (la amuna ndi akazi), akatswiri a Sayansi amadziwa bwino kuti pali kusiyana kovuta

CONTENTS




kukumvetsa pa momwe nzeru za amuna ndi akazi zimaunikira chiyankhulo, nkhani ndi chikhalidwe, kungotchulako zochepa chabe.

Katswiri wa za chikhalidwe cha anthu ndi wofufuza za zinthu za moyo, Edward O. Wilson wa ku Sukulu ya ukachenjede ya Harvard, adafotokoza kuti, akazi ali opambana zedi kuposa amuna pa maluso akayankhulidwe, chisoni, ndi kulumikizana bwino ndi anthu a m'dera, mwa zina. Pamene amuna ndiye ali opambana zedi pa kudzidarira, kugonjetsa, maluso a zamasamu, okonda udindo, ukali ndi mbiri zina zotero.

Zingathe kukhala zopanda nzeru kuchita nawo onse awiriwa (amuna ndi akazi) mofanana, ndi kusalabadira kusiyana kwawo. Chisilamu chimatiphunzitsa kuti amuna ndi akazi ndiamodzi, koma ali ndi ma udindo osiyana oyenererana ndi chilengedwe chawo. Mulungu (Allah) akuti:

*"Ndipo wamwamuna saali ngati wachikazi"*

Qur'an 3:36

*"Kodi asadziwe amene adalenga (zinthu zonse)? Pomwe Iye Ngodziwa zinthu zing'onozing'ono kwambiri m'mene zilili, (ndiponso) Ngodziwa nkhani zonse."*

Qur'an 67:14

## UMODZI WA BANJA

Mulungu (Allah) adalenga mamuna ndi mkazi kuti akhale osafanana, okhala ndi ntchito, maluso ndi ma udindonso osiyana. Kusiyana kumeneku sikutengedwa ngati umboni wowonetsa kulemekezeka ndi kunyozeka, koma ndichinthu chongosonyeza mbali yomwe adamusankhira aliyense mwa awiriwa. Ku Chisilamu, banja lili ndi kufunikira kwakulu. Mamuna ali ndi udindo wa kuyendetsa bwino nkhani zachuma pabanja, pomwe mkazi amatenga gawo la kukhala bwino kwa zakuthupi, zamaphunziro ndi kamvedwe kabwino ka m'mitima ndi m'nzeru ka anthu onse pabanjapo. Izi zimalimbikitsa kumvana (pakati pawo) m'malo mwa kupikisana. Pokwaniritsa maudindo awo, mabanja amphamvu amakhazikitsidwa, ndipo zotsatira zake midzinso yamphamvu imamangidwa.

Komanso, amuna ngakhalenso akazi, onsewa sangakhale moyo wosangalala m'maganizo ndi mumtima mwawo popanda wina ndi nzake. Mulungu (Allah) akufotokoza zimenezi mochititsa kasu ponena kuti:

*"Iwo ali ngati chovala chanu. Inunso muli ngati chovala chawo"*

Qur'an 2:187

Chovala chimapereka mtendere, kutenthera ndi chitetezo, komanso kumpangitsa munthu kuoneka bwino – m'menemo ndi m'mene ubale pakati pa mamuna ndi mkazi umafotokozeredwa m'Chisilamu.

CONTENTS
































# CHIKONDI NDI CHISONI MU UBALE WA PABANJA

Mneneri (mtendere ukhale pa Iye) nayenso ankalimbikitsa amuna kuti azikhala ndi akazi awo ndi chikhalidwe chabwino, "Abwino mwa inu ndi amene amakhala abwino kwa akazi awo." Sahih (Tirmidhy: 3895)

*"Ndipo zina mwa zizindikiro zake (zoonetsa chifundo chake kwa inu) ndiko kukulengerani akazi a mtundu wanu kuti mukhazikike (mitima yanu) kwa iwo, ndipo adaika pakati panu chikondi ndi chisoni. Ndithu mzimenezi muli zizindikiro kwa anthu amene amalingalira."*

Qur'an 30:21

Aisha (mkazi wa mtumiki) adafunsidwapo za mmene Mtumiki amakhalira m'nyumba mwake. Iye adati "Ankakhala ngati mmodzi wa inu m'nyumba mwake, anali wodekha kwambiri, komanso wothandiza zedi.....Ankakhala wokonzeka kupereka chithandizo kwa akazi ake mu ntchito wamba za pakhomo, amasoka zovala zake ndi nsapato zake (zikang'ambika)". Sahih (Ahmad: 25341). Mwachidule, Iye ankathandizira pa ntchito iliyonse yomwe akazi ake ankachita.

# UDINDO WAPAMWAMBA WA AMAYI NDI ANA (ACHIKAZI)

Mai ali ndi mphamvu yomusintha mwana makamaka mu zaka zake zoyambirira, kupyolera m'chisamaliro ndi chikondi chawo. Mosakaika, kupambana kwa dera ndi chifukwa cha amayi. Kwa ichi, kumayeneradi kuti Chisilamu chiwalemekeze ndi kuwakweza nyota yawo.

Allah akuyankhula m'Qur'an:

*"Ndipo tamulangiza munthu kuchitira zabwino makolo ake. Mayi wake adatenga pathupi pake mwamasautso."*

Qur'an 46:15

Mtumiki (mtendere ukhale pa Iye) adafunsidwapo (kuti), "E, Mtumiki wa Allah, ndindani mwa anthu amene akuyenera zedi kumuchitira zabwino?". Iye adati, "Amayi ako." Munthu adafunsa kachiwiri: "Kenako ndani?" Ndipo amapatsidwa yankho limodzimodzi. Mpakana kachinayi ndipamene Mtumiki adayankha kuti, "Kenako bambo ako." Sahih (Al Bukhari: 5971)

Sikuti malipiro amangoperekedwa powachitira zabwino amayi wokha ayi, koma Chisilamu chidakhazikitsanso malipiro apadera chifukwa cha kumulera mwaubwino mwana wamkazi, omwe sadaperekedwe pomulera mwana wamamuna.

Mtumiki wa Allah (mtendere ukhale pa Iye) adati, "Amene Allah wamupatsa ana awiri achikazi choncho iye akuchita zabwino pa iwo, iwowo adzakhala chifukwa chokamulowetsa ku Paradiso." (Ahmad:11384)

CONTENTS


























# KUMALIZA

Chisilamu chisanabwere, akazi amatengedwa ngati chinthu chochititsa manyazi, ana aakazi amakwiriridwa m'dothi ali amoyo, kuthetsa banja kunali m'manja mwa mamuna yekha basi, chuma chamasiye chinkatengedwa ndi amphamvu okha basi, ndipo kupondereza kunali ponseponse. Chisilamu chinabwera ndipo chinathetsa machitidwe amenewa. Ngakhalenso pakadali pano, "m'maiko otukukuka", akazi alibe ufulu wawo oyenerera. Koma Chisilamu, chimawatenga akazi kuti ndi ofunikira komanso amtengo wapatali, omwe sakuyenera kusalemekezedwa ndi kunyozedwa. Kuchitiridwa zoipa kumene akuchitiridwa akazi m'maiko ena a pakati pa kummawa (omwe ndi maiko a maArabu ndi amwenye), kapena m'mabanja ena, kumachitika chifukwa cha miyambo ya zikhalidwe zina zimene Asilamu amazitsatira molakwika, osati chifukwa cha Chisilamu ayi. N'chifukwa chiyani akazi ambiri mwaufulu wawo akulowa Chisilamu ngati chili chipembedzo chopondereza?

Tikumaliza ndi mawu a Mbuye wathu ndi Mbuye wanu, Mlengi ndi Msamali wa amuna onse ndi akazi onse:

*"Ndithu Asilamu achimuna ogonjera Allah mokwanira, ndi Asilamu achikazi ogonjera Allah mokwanira, okhulupirira achimuna ndi okhulupirira achikazi, omvera achimuna ndi omvera achikazi, oona achimuna ndi oona achikazi, opirira achimuna ndi opirira achikazi, odzichepetsa achimamuna ndi odzichepetsa achikazi, opereka chopereka chaulere achimuna ndi opereka chopereka chaulere achikazi, osala (chakudya) achimuna ndi osala achikazi, osunga umaliseche wawo (kuchiwerewere) achimuna ndi osunga umaliseche wawo achikazi, otamanda Allah kwambiri achimuna ndi otamanda Allah kwambiri achikazi, Allah wawakonzera chikhululuko ndi malipiro aakulu."*


Qur'an 33:35

CONTENTS































# KUSAKHULUPIRIRA MLENGI

## M'KAYANG'ANIDWE KA CHISILAMU

CHICHEWA (MALAWI) (09/11) الإلحاد FREE COPY



*"Posachedwapa tiwaonetsa (awa okanira), zisonyezo zathu kumbali zonse (za dziko), ndi mwa iwo eni kufikira zionekere kwa iwo kuti chimene wadza nachochi nchoona".*


Quran 41:53


Dar Al Ber Society
www.daralber.ae
الإمارات THE EMIRATES
Your Path To Peace..
مركز المعلومات الإسلامي
Islamic Information Center
للتعريف بالإسلام
تصريح رقم: (2017/139)
دائرة الشؤون الإسلامية والعمل الخيري
Islamic Affairs & Charitable Activities Department
www.islamicic.com

CONTENTS
























Kabuku aka kakufotokoza za kawonedwe ka Chisilamu pankhani ya kukhulupirira mwa Mlengi. Kakufotokoza momwe Allah amaperekera zisonyezo (zosonyeza) kupezeka kwake – kuyambira kudzera mu zolengedwa zake komanso kudzera mu chivumbulutso, ndipo kakufotokoza momveka bwino mafunso otchuka a anthu osakhulupirira Allah.

Allah, kupyolera m'zizindikiro zake akutiitanira kuti tikhulupirire za kupezeka kwake, ndipo watipatsa udindo wa kulingalira kuti tithe kumuzindikira ndi kumudziwa. Choncho ena mwa anthu amakhulupirira kupyolera mu zomwe akuziona ponse ponse zochokera mu zisonyezo ndi ntchito zake. Pomwe ena amakanira ndi kuzitaya zonsezi kuti zilibe tanthauzo lililonse. Allah adakhazikitsa mwa munthu aliyense chibadwi ndi mtima wakukhulupirira, chabe kuti chibadwi chimenechi chingathe kulimbikitsidwa kapena kuchotsedwa ndi kufafanizidwa.

> *N'kofunikira kudziwa kuti Allah amawatsogolera kuti alandire chiwongoko amene ali ndi mtima wofunisitsa ndi wofunitsitsa. Kutanthauza kuti amene sakufuna kukhulupirira mwa Allah satsogoleredwa.*
>
> *Allah akuyankhula kuti: "Ndipo (Allah) amamuongolera amene akutembenukira kwa Iye."*
>
> Quran 13:27

Zimenezi zikukakamiza kuti yemwe akutsutsa za kupezeka kwa Allah akhale ndi mtima wachilungamo, wosakondera ndi wosadzisankhirathu mbali yomwe ikumukomera, pamene akuyang'ana nkhani ya kupezeka kwa Allah. Ndi kuti asachitenge chinthu chimenechi kuti n'chosatheka kapena chopanda pake. Ndipo popanda mtima ngati umenewu n'kosatheka kukhulupirira ngakhale munthuyo atakhala ndi maphunziro ochuluka motani. Ndipo Allah wachenjeza kuti anthu amene amadzikweza posafuna kulandira zisonyezo zake, akapeza chilango choyenerana ndi kukanira kwawoko.

> *N'kofunikiranso kufotokoza kuti chifukwa cha kusiyana kwakulu komwe kulipo pakati pa Chisilamu ndi Chikhirisitu pankhani yokhudza chikhulupiriro mwa Allah, zitozo zambiri zomwe zili ku Chikhirisitu sizipezeka kapena kuperekedwa ku Chisilamu.*

Choncho ndi chiyembekezo chathu kuti iwo amene ali ndi mtima oyera ndi wotseguka, ndiponso ndiofunitsitsa kuchidziwa choonadi, apindula ndi nkhani iyi. Ndi kuti zithandizira kupereka kamvetsetsedwe katsopano pankhani ya Allah.

# ZIFUKWA ZOCHITITSA KUTI TIKHULUPIRIRE

M'musimu muli zifukwa zitatu zanzeru zochititsa kuti tikhulupirire za kupezeka kwa Mlengi.

## 1. CHIYAMBI CHA DZIKO

Umboni woyamba womwe ukusonyeza kuti kuli Mlengi, ukukhudzana ndi kumvetsetsa bwino za chiyambi cha dzikoli.

Tangoyerekeza kuti uli mkati moyenda ku chipululu waipeza wotchi. Tonse tikudziwa kuti wotchi imawumbidwa ndi galasi, pulasitiki ndi chitsulo. Galasi limachokera ku mchenga, pomwe pulasitiki amachokera ku mafuta, ndipo chitsulo chimachokera ku nthaka; zinthu zonsezi zimapezeka ku chipululu. Kodi iweyo ungakhulupirire kuti wotchiyi idadzipanga yokha?

CONTENTS






*'Kapena adalengedwa popanda Mlengi kapena iwo adadzilenga okha?'.*

**Quran 52:35-6**

Kuti dzuwa lidawala, mphepo n'kuwomba, mphenzi n'kumenya, mafuta n'kukhovokera pamwamba pa nthaka, ndi kusanganikirana ndi mchenga ndi chitsulo chija, ndipo kenako patapita zaka miyandamiyanda wotchi n'kuwumbika yokha mwachilengedwe?

Malingana ndi Sayansi yamakono, ikutiwuza kuti dziko lili ndi chiyambi. Kodi dzikoli lidachokera kuti? Malingana ndi chizolowezi ndi nzeru za munthu wina aliyense (popanda kusaukira kukhala ndi maphunziro ambiri), timadziwa kuti chilichonse chimene chili ndi chiyambi sichingangoyamba chokhachokha popanda wochiyambitsa, ndipo sichingadzilenge chokha. Choncho mfundo yomveka ndi yotsimikizika ndiyakuti pali wina wake yemwe adalenga dzikoli. Mlengi ameneyu akuyenera kukhala Wamphamvu ndi Waluntha kotero kuti adakwanitsa kuchibweretsa chidziko chonsechi kukhala chinthu chopezeka, nalenga malamuro a zachilengedwe (Sayansi) omwe akuyendetsa dzikoli. Mlengi ameneyu akuyeneranso kukhala wosasawukira nthawi ndi malo, pakuti zonsezi zidayamba pamene dziko lidalengedwa. Mfundo zonsezi zikumanga phata la chikhulupiriro chakuti kuli Mlengi.

Ena angathe kufunsa kuti: 'Kodi ndani amene adamulenga Mlengiyo?'

Allah yemwe ndi Mlengi, Ndiwosafanana ndi zolengedwa zake. Allah Ndiwamuyaya, adalipo nthawi zonse ndipo kupezeka kwake kulibe mathero. Choncho kufunsa kuti 'adamulenga Allah ndi ndani', limeneli ndi funso lopanda nzeru.

## 2. KUKWANIRA BWINO KWA DZIKO

Tsono umboni wachiwiri wosonyeza kuti Mlengi alipodi, ndi ndondomeko ndi kulingana bwino kwa chidziko chododometsa m'kakhalidwechi.

Zingatheke chidziko chachikulu chododometsa ngati ichi kudzilenga chokha, popanda uyang'aniri ndi utsogoleri wa wina wake wamphamvu ndi waluntha lopanda malire?

Magawo ambiri m'chidziko chimenechi amaonetserathu poyera kuti chidakonzedwa ndicholinga chothandizira moyo. Zinthu monga ngati kutalikirana kwa dziko lathuli ndi dzuwa, kukula kwa mphipi ya nthaka, mulingo wa liwilo lomwe dziko lathuli limathamangira pozungulira, mulingo wa mpweya wopumira mu mlengalenga (oxygen), ngakhalenso kapendekedwe ka dzikoli ndi zina. Kapimidwe ka milingo imeneyi kakadati kasiyane pang'ono chabe ndi momwe kalili pakadali pano, moyo padziko pano sukadapezeka.

Choncho ngati momwe zilili kuti wotchi ili ndi amene adaikonza kuti idzisunga nthawi bwino bwino, chimodzimodzinso dzikoli lili ndi Mkozi wake Wanzeru kuti lidziyenda bwino bwino m'njira yake popanda kuphonya. Kodi n'zotheka zimenezi kuchitika mwa izo zokha?

Pamene tikuona ndondomeko zokhazikika mwa ife eni komanso padziko lonse, kodi sizingakhale zanzeru kunena kuti zili ndi amene adazikonza? Ndipo kumufotokoza kwabwino zedi Mkonzi ameneyu ndiko kukhulupirira kuti Allah alipo, amene adabweretsa ndondomeko zimenezi.


N'koyenera kudziwa kuti Chisilamu chimalimbikitsa ufufuzi wa Sayansi ndi kulingalira. Ntchito ya Sayansi ndiyakuti imatatinthandizira kufotokozera bwino mitundu yosiyanasiyana ya ndondomeko zimene Allah amaika mu zolengedwa zake, ndi kutinso tiyamikire ndi kuzindikira bwino kukula kwa mphamvu ndi luntha lake. Kupita patsogolo pa uzindikira wa Sayansi, monga ngati zidango-dango kapena zochitika zodabwitsa zomwe zimachitika m'dzikoli; monga ndondomeko ya kayendedwe ka madzi (water cycle) ndi zina zangati zimenezi, zimapereka zisonyezo zakuti pali Mlengi ndi Mkonzi, osati kuti tipezerepo mtsutso wakuti Mlengi kulibe ayi.

CONTENTS
































# 3. CHIVUMBULUTSO KUCHOKERA KWA ALLAH

Umboni wachitatu, ndi chivumbulutso chomwe Allah adapereka kwa anthu ngati chisonyezo chakuti Iye alipodi.

Chimodzi mwa zolinga zikulu-zikulu za buku la Chisilamu (Qur'an), ndicho kuwaitanira anthu kuti alingalire ndi kuyamikira za chilengedwe cha Allah, ngati njira imodzi ya kumukhulupirira. M'Qur'an yonse, Allah akuitanira kuti tipereke chidwi chathu ku kakonzedwe ndi kawumbidwe kake kododometsa ndi kochititsa kasu m'dzikoli, zomwe zikukwanira kutiwonetsa kuti ndife zotsatira za kukonza kwake, zolinga zake ndi luntha lake. Mwachitsanzo, Allah akunena kuti:

> ***Ndithudi, m'chilengedwe cha thambo ndi nthaka, ndi kusinthana-sinthana kwa usiku ndi usana, ndi zombo zikulu-zikulu zomwe zikuyenda panyanja (zitasenza zinthu) zothandiza anthu, ndi madzi amene Allah wawatsitsa kuchokera kumitambo, naukitsira nawo nthaka pambuyo pokhala yowuma, nawanditsa m'menemo mtundu uliwonse wa nyama (chifukwa cha madziwo), ndi m'kusinthanasinthana kwa mphepo, ndi mitambo yomwe yalamulidwa kuyenda pakati pa thambo ndi nthaka; ndithudi, (m'zimenezo) muli zisonyezo kwa anthu anzeru (kuti Allah alipo).***
>
> Quran 2:164

Kuwonjezera apo, pali zizindikiro zowonekera poyera zosonyeza kuti Qur'an ndi mawu a Allah.

## QUR'AN:

*Qur'an idalowezedwa ndi asilamu miyanda-miyanda, yonse kumayambiriro mpaka kumapeto.*

- Ndiyotetezeka ku zolakwika kapena zotsutsana zilizonse.
- Idasungidwa lemba ndi lemba m'chiyankhulo chake cheni-cheni chachiarabu kuchokera nthawi ya kuvumbulutsidwa kwake, kusiyana ndi mabuku ena.
- Ili ndi uthenga wosavuta, woyera ndi woyenera anthu a mitundu yonse omwe umaitanira nzeru za munthu ndi chikhulupiriro chake chachibadwa ku kukhulupirira mwa Allah.
- Ladutsa zaka zoposa 1400 lili ndi mfundo zambiri-mbiri zotsimikizika zasayansi, zomwe sizinkadziwika kwa wanthu a nthawi zimenezo, ndipo zangotulukilidwa posachedwapa ndi Akatswiri a Sayansi. Zina mwazitsanzo ndi izi: 'Madzi ndi tsinde la chiyambi cha moyo wa zinthu zonse (Qur'an21:30); 'Dzikoli likutambasuka ndi kukula' (Qur'an51:47); ndi 'Kuyenda mozungulira kwa dzuwa ndi mwezi' (Qur'an 21:33).
- Lili ndi mfundo zotsimikizika za histole (mbiri) zomwe sizinkadziwika kwa anthu a nthawiyo, komanso lili ndi maulosi ankhani-nkhani omwe atsimikizika kuti ndi owonadi.
- Idavumbulitsidwa kwa Mneneri Muhammad (mtendere ukhale pa Iye) yemwe amadziwika kuti ndi wosadziwa kulemba ndi kuwerenga, chikhalirecho lili ndi chiyankhulo chozama mwapadera-dera, kotero kuti imadziwika padziko lonse kuti ndi tsinde la chiarabu chomveka bwino ndi chiyankhulo chokongola.

*Qur'an ili ndi mphamvu yakuya ndi yaikulu pa (kusintha) miyoyo ya wanthu.*

Kafotokozedwe kogwirizana zedi ndi nzeru ka zodabwitsa ndi zozizwitsa zankhani-nkhani za Qur'an, nkakuti bukuli likuyenera kuchokera kwa Allah basi, palibenso china.

CONTENTS
























# MAFUNSO OKHUDZA ALLAH

## "N'CHIFUKWA CHIANI ALLAH ADATILENGA?"

Aliyense angathe kuvomereza kuti ziwalo za thupi lathu monga maso, makutu, ubongo ndi mtima, zonsezi zili ndi cholinga chake. Kodi sizingakhalenso zanzeru kuti munthu yenseyo (watunthu) alinso ndi cholinga?

Allah, Wanzeru zonse, sadatilenge kuti tidzingoyumba-yumba popanda cholinga, kapena kuti tingokwaniritsa zilakolako zathu zachilengedwe basi. Koma Allah akuwusimba moyowu kuti ndi mayeso. Munthu aliyense akuyesedwa kuti adziwike amene asankhe kumuvomereza Allah ndi kutsatira chiwongoko chake. Allah akuti:

*"Ndithu Ife tidamlenga munthu kuchokera ku mbewu ya munthu yosakanikirana (ya mkazi ndi mamuna) kuti timuyese mayeso (ndi malamulo athu); choncho tidampanga kukhala wakumva ndi wopenya. Ife tidamlongosolera njira yowongoka: kukhala wokhulupirira kapena wotsutsa".*

Quran 76:2-3

Kwa anthu ambiri nkhani yaikulu sikukhulupirira mwa Allah kokhako ayi, koma vuto limakhala pa zotsatira pambuyo pa chikhulupirirocho. Chifukwa, kwai wo zimatanthauza kuti akuyenera kukafunsidwa ndi kuweruzidwa pa zomwe adali kuchita, zomwe amaziona kuti zisokoneza moyo umene amafuna azikhala pano padziko. Choncho mayeso pano padziko agona pa kudzichepetsa tokha kwa Allah, ndi kugonjera malamulo ake, ndi kusiya zilakolako ndi zofuna za mitima yathu.

## "KODI ALLAH AMASAWUKIRA KUTIYESA IFE?"

Allah Sali Wosawukira chilichonse. Sasawukira kulenga chilichonse ndiponso sasawukira kumuyesa aliyense.

Iye sapindula kalikonse pa kukhulupirira kwathu komanso sakhudzika chifukwa cha kusakhulupirira kwathu. Koma kuti ndi mbali imodzi ya luntha lake kuti adatilenga ndikutipatsa mwayi wakuti timudziwe, ndipo Iye adadziwirathu zamtsogolo. Koma mfundo yaikulu ndiyakuti, ifeyo tikhale mmoyo uno ndi kuchita zisankho zathu, osati kuti Allah ali Wosawukira kutiyesa kapena ayi.

## "KOMA NDIZOONA KUTI TILI NDI UFULU?"

Pamene tikunena kuti Allah adadziwa kale za chisankho chathu, sizikitanthauza kuti tilibe ufulu wa kusankha. Ngakhale kuti Allah amafuna kuti anthu amkhulupirire, komabe sachita mowakakamiza ayi. Allah akadafuna akadawaongolera anthu onse kuchiwongoko chifukwa Iye ali ndi mphamvu zotha kuchita chilichonse. Koma mwaluntha lake, adatilenga ndi mphamvu yakutha kusankha, ndipo watipanga kukhala ndi udindo wokayankha pa zisankho zathu. Allah sikuti amasangalala ndi zonse zomwe amalola kuti zichitike padziko.

## "BWANJI ALLAH SAWONEKERA KWA ANTHU?"

Malingana ndi luntha lake Allah, adasankha kuti tizimudziwa kupyolera m'zisonyezo zake ndi ntchito zake. Limeneli ndi gawo la mayeso m'moyo uno.


Iye waupanga kukhala udindo wathu kugwiritsira ntchito maluso ndi mphamvu zomwe Iye adatipatsa kuti timuzindikire.

CONTENTS
































## 'N'CHIFUKWA CHIANI PADZIKO PALI MASAWUTSO?'

Ngakhale kuti kuyesedwa kwa anthu padziko lino kumasiyana-siyana, izi sizitanthauza kuti Allah kulibe, ndiponso sizitsutsana ndi mphamvu zake ndi kutha kwake.

Koma kuti, zabwino ndi zoipa zomwe zimachitika padzikoli mwachilolezo cha Allah, ndi mbali imodzi ya kuyesedwa kwathu pano padziko. Inde, tilibe mphamvu iliyonse pa zomwe zimachitikira, koma tili ndi mphamvu ya momwe tingachitire pamene zatipeza (popirira kapena kusapirira, kukhulupirira kapena kukanira). Zimenezi ndi zomwe Allah amayang'ana pa ife ndi kutiweruza nazo moyenerera. Dzikoli ndilongoyembekezera chabe, ndipo m'moyo womwe uli nkudza – womwe ndiwopitirira ndi wamuyaya - , kumeneko ndikomwe mzimu uliwonse ukalipidwa mokwanira ndi moyenera pa zomwe unkachita.

## 'N'CHIFUKWA CHIANI ALLAH AMAWALANGA ANTHU?'

Palibe amene angatsutse za nkhani ya chilango, chomwe ndi chinthu choyenerera pofuna kukwaniritsa chilungamo. Allah adatilenga ndi mphamvu yakutha kusankha moyo umene tikufuna kukhala pano padziko, ndipo tikafunsidwa molingana ndi chisankho chathucho.

Choncho amene akulimbikira mwachoonadi pomugonjera Allah, adzapeza chisomo cha Allah nalowa ku munda wamtendere. Koma amene sasamala za cholinga cha moyo wawo namukana Allah, nawonso adzipangira chisankho chawo ndipo akaweruzidwa moyenerera. Allah sadawalenge anthu kuti akawalange, koma Iye nthawi zonse amawafunira zofewa ndi chifundo. Choncho pamene tikunena kuti Allah amadziwa bwino zisankho zathu, izi sizikutanthauza kuti tilibe ufulu wosankha pa zochita zathu, ndiponso sizikutipanga kukhala opanda udindo uliwonse pa ntchito zathuzo.

Chisilamu ndi chipembedzo chotheka kuchigwiritsira ntchito, ndipo chimatilimbikitsa kukhala pakati pa chiyembekezo mu chifundo cha Allah, ndi kuwopa chilango chake. Zinthu ziwirizi ndizofunikira kuti munthu akhale ndi moyo wabwino ndi wodzichepetsa. Allah Ngwachifundo chambiri, komanso nthawi yomweyo Ngwachilungamo. Choncho zikanakhala kuti palibe tsiku lachiweruzo, ndiyekuti zikadatsutsana ndi chilungamo chake chokwanira, ndipo moyowu ukadakhala wopanda tanthauzo.

## KUMALIZA

Kodi tikhala padziko pano zaka 80 kapena kuposera apo, n'kuthera pompo basi? Kapena pali china chake chachikulu choti tipeze m'moyowu?

Kodi ifeyo ndiankhwere chabe otukuka mu zochita zathu, amene tilibe cholinga chilichonse (ngati momwe anthu a Sayansi amanenera)? Kodi ndife zinthu zamoyo zongokhala ndi zilako-lako za thupi, kapena tilinso ndi zosawukira kumbali ya uzimu?

Kwa amene ali ndi mtima weni-weni ndipo sadapangebe chiganizo bwino-bwino pankhani ya Allah, langizo lathu kwa iwo ndilakuti apemphe pempho lotsatirali mwachoonadi:

**'E, Inu Allah! Ngati Inu mulipodi ndiye chonde ndiwongolereni.'** Mudzakhala wodwaba pa zotsatira za zimenezi!

HOTLINE
+971 56 204 2045
islamicicdxb
islamicic.com info@islamicic.com +971 4 355 5223
DOWNLOAD CHICHEWA FLYER
www.iicdxb.com/chichewa

CONTENTS

MAU OTSEGULIRA OFOTOKOZA CHISILAMU
MTUMIKI MUHAMMAD MTENDERE UKHALE PA IYE
YESU: MTHENGA WA MULUNGU (ALLAH)
MULUNGU M'CHISILAMU
KORANI
KODI CHOLINGA CHA MOYO NDI CHIANI?
KUCHIMVA MOLAKWIKA CHISILAMU
UFULU WA AKAZI M'CHISILAMU
KUSAKHULUPIRIRA MLENGI M'KAYANG'ANIDWE KA CHISILAMU
ZOZIZWITSA ZASAYANSI MU QUR'AN

# ZOZIZWITSA ZASAYANSI MU QUR'AN

CHICHEWA (MALAWI) (10/11) العلوم في الإسلام FREE COPY

*'Posachedwapa tiwaonetsa (awa okanira), zisonyezo zathu kumbali (zonse) za dziko ndi mwa iwo eni, kufikira zionekere kwa iwo kuti chimene wadza nachochi n'choona?'*

Quran 41:53



جمعية دار البر
Dar Al Ber Society
www.daralber.ae

الإمارات
THE EMIRATES

*Your Path To Peace..*

مركز المعلومات الإسلامي
Islamic Information Center
للتعريف بالإسلام

تصريح رقم:
(2017/139)

دائرة الشؤون الإسلامية والعمل الخيري
Islamic Affairs & Charitable Activities Department


www.islamicic.com

CONTENTS

































Qur'an, buku la Chisilamu, ndi buku lomaliza la chivumbulutso cha Allah kwa mtundu wa anthu, komanso ndi lomaliza mu m'ndandanda wa zivumbulutso zomwe zidaperekedwa kwa aneneri.

Ngakhale kuti Qur'an (yomwe idavumbulitsidwa zaka 1400 zapitazo) sibuku la sayansi, koma mkati mwake lili ndi mfundo zotsimikizika za sayansi zimene zangotulukilidwa kumene kupyolera mu kupita patsogolo kwa tekinoloje ndi maphunziro a sayansi. Chisilamu chimalimbikitsa kulingalira ndi kufufuzi kupyolera mu Sayansi chifukwa chakuti kuchimvetsetsa chilengedwe kumawathandizira anthu kuyamikira Mlengi wawo ndi kuzindikira kuya kwa mphamvu zake ndi luntha lake.

Qur'an idavumbulutsidwa mu nthawi imene Sayansi idali yapansi zedi; kudalibe matelesikopu (zida zoyang'anira zinthu zomwe zili kutali), mayikolosikopu (zida zoyang'anira zinthu zazing'ono zedi zosatheka kuoneka ndi maso chabe), kapena chilichonse chofanana ndi ukadawulo wa tekinoloje ya lero lino. Anthu ankakhulupirira kuti dzuwa ndi limene limalizungulira dziko, ndi kuti thambo lanyamulidwa ndi mapilala amene ali m'makona a dzikoli lomwe ndi lolingana (lafulati). Koma motsutsana ndi kubwerera m'mbuyo kumeneku, Qur'an idavumbulitsidwa ndipo idasonkhanitsa mkati mwake mfundo zotsimikizika za Sayansi pa mitu yosiyanasiyana kuyambira Astronomy (phunziro lofufuza za zinthu za mmalengalenga monga nyenyezi, mapulaneti ndi zina); kukafika ku nkhani za Biology (phunziro lofufuza za zinthu za moyo monga anthu, nyama ndi zina); Geology (phunziro lofufuza za zinthu za mkati mwa nthaka monga miyala ndi zina); Zoology (phunziro lofufuza za nyama, mitundu yake, chibadwi chake ndi zikhalidwe zake).

Zina mwa mfundo zotsimikizika za Sayansi zomwe zili mQur'an ndi izi:

## 1 Chiyambi cha Moyo

Madzi atchulidwa kuti ndi tsinde la chiyambi cha moyo. Zamoyo zonse zimapangidwa kuchokera ku ma cells (tizidutswa ting'ono-ting'ono tomwe cholengedwa chilichonse chimawumbidwa posonkhanitsa timeneti), ndipo lero lino tadziwa kuti ma cells amenewa nthawi zambiri amapangidwa kuchokera ku madzi.

> *"Ndipo ndi madzi tidalenga chilichonse chamoyo. Kodi sakukhulupirira?"*
> **Quran 21:30**

Zimenezi zinazindikiridwa pambuyo pa kupangidwa kwa chida cha microscope (maikoloskopu). Choncho sichingakhale chanzeru kuganizira kuti wina wake ku chipululu cha Arebiya adangochita molota kuti moyo udachokera ku madzi.

## 2 Kukula kwa munthu m'chiberekero

Allah akuyankhula za milingo yosiyanasiyana ya moyo wa munthu m'chiberekero.

> ***"Ndipo ndithu, tidamlenga munthu kuchokera ku dongo labwino. Kenako tidampanga kukhala dontho la madzi lomwe lidaikidwa pamalo osungidwa. Kenako tidalisintha dontholo kukhala alaqah (chinthu chokhala ngati nsundu, chinthu cholendewera, ndi magazi owundana). Ndipo kenako tidaipanga alaqah kukhala mudghah (chinthu chokhala ngati chotafunidwa).***
> **Quran, 23:12-14**

Liwu lachiarabu loti "alaqah" lili ndi matanthauzo atatu: nsundu, chinthu cholendewera ndi magazi owundana. "Mudghah" imatanthauza chinthu chotafunidwa. Akatswiri a Sayansi yowunika za moyo wa munthu m'chiberekero adapeza kuti kugwiritsira ntchito mawu amenewa pofotokoza za kuwumbidwa kwa munthu m'chiberekero ndi kolondola zedi ndipo kukugwirizana mwamtheradi ndi ufufuzi wa Sayansi ya makono pankhani ya moyo wa munthu m'chiberekero.

CONTENTS






Ndizochepa zedi zomwe zimadziwika zokhudza milingo ndi magawo osiyana-siyana a munthu m'chiberekero kufikira senchale ya makumi awiri (zaka 100 zapitazo), zomwe zikutanthauza kuti kufotokoza kwa Qur'an za moyo wa munthu m'chiberekero sikudachitike podalira maphunziro a Sayansi kuchokera mu senchale ya chisanu nchiwiri 700C.E (zaka 1300 zapitazo).

## 3 Kutambasulidwa kwa Dziko

Mu nthawi imene Sayansi ya zinthu za m'malengalenga idali yapansi zedi, ndime yotsatirayi idavumbulitsidwa m'Qur'an:

*'Ndipo mlenga-lenga tidawumanga mwamphamvu ndipo Ife tili Owutambasula (kuwukuza).*

**Quran 51:47**

Limodzi mwa matanthauzo a ndime imeneyi ndilakuti Allah akumalikulitsa ndi kulitambasula dzikoli (kutanthauza kumwambaku). Matanthauzo ena ndiakuti; Allah amapereka zofunikira, ndiponso ali ndi mphamvu pa dziko lonseli – onsewa ndi matanthauzo olondola.

Mfundo yonena kuti dzikoli likutambasuka ndi kukula (mwachitsanzo: mapulaneti akutalikirana-talikirana), mfundo imeneyi idatulukiridwa mu senchale yapitayi (zaka 100 zapitazo). Katswiri wa Sayansi dzina lake Stephen Hawking adalemba m'buku lake lotchedwa 'Mbiri yachidule ya nthawi,' kuti;

"Kutulikira ndi kuzindikira zonena kuti dzikoli likutambasuka chinali chimodzi mwa zinthu zikulu-zikulu zomwe zasintha uzindikiri wozama mu senchale ya makumi awiri".

Qur'an yalozera za kutambasuka kwa dzikoli ngakhale chida cha telescope (chowunikira zinthu zomwe zili kutali) chisanapezeke nkomwe.

## 4 Chitsulo Chidatsitsidwa

Chitsulo sichidapezeke m'nthaka mwachilengedwe kuchokera pachiyambi, koma chidachita kubwera kuchokera kunja kwa dziko lokhalamo anthu lino. Akatswiri a Sayansi adatulukira kuti zaka miyanda-miyanda zapitazo dzikoli lidamenyedwa ndi zidutswa za zitsulo zochokera ku nyenyezi zomwe zidaphulika ku milenga-lenga

*"Ndipo tidatsitsa chitsulo momwe muli mphamvu zambiri (pankhondo) ndiponso chithandizo kwa anthu..."*

**Quran 57:25**

Allah wagwiritsira ntchito mawu akuti 'tidatsitsa'. Nkhani yonena kuti chitsulo chidatsitsidwa kuchokera ku milenga-lenga ndi chinthu chimene Sayansi yotsalira ya zaka za m'ma 700 C.E siikadatha kuizindikira.

## 5 Chitetezo cha mlenga-lenga

Mlenga-lenga umagwira ntchito yofunikira zedi politeteza dziko lokhalamo anthu lino ndi zonse zokhala m'menemo, kuchokera ku kutentha kowopsya kwa dzuwa, komanso kuzizira kwa mnanu kochokera kumwamba.

M'ndime yotsatirayi Allah akutiwuza kuti tilingalire za mlenga-lenga:

"Ndipo thambo tidalipanga kukhala denga loteteza, koma iwo akuzitembenukira kumbali zizindikiro zake". [Quran 21:32]

Qur'an ikulozera kuti chitetezo cha mlenga-lenga ndi chisonyezo cha Allah, zidango-dango za chitetezo zomwe zidatulukiridwa kupyolera mu ufufuzi wa Sayansi omwe udachitika mu senchale ya makumi awiri (zaka 100 zapitazo).

CONTENTS







## 6 Mapiri

Allah akutiwuza kuti tipereke chidwi chathu pa chikhalidwe chofunikira zedi cha mapiri:

> *"Kodi sitidachite nthaka kukhala ngati choyala? Ndi mapiri ngati zichiri (zolimbitsa nthaka)?*
>
> **Quran 78:6-7**

Qur'an molondola zedi yayisimba mizu yakuya ya mapiri pogwiritsira ntchito mawu akuti "zichiri". Phiri la Everest, mwachitsanzo ndilalitali pafupi-fupi 9 kilomita kupita m'mwamba, pomwe tsinde lake ndilalitali makilomita 125 kupita pansi!

Mfundo yakuti mapiri ali ndi mizu yokhala ngati zichiri (misomali), siimadziwika kufikira pamene kunabadwa phunziro lotchedwa "plate tectonics" (lomwe ndi phunziro lofufuza mbali zosiyana-siyana za gawo la pamwamba pa nthaka), kumayambiriro kwa senchale ya makumi awiri (zaka 100 zapitazo). Allah akunenanso mu Qur'an kuti mapiri ali ndi ntchito yolimbitsa nthaka "......kuti isakugwedezeni," zomwenso akatswiri a Sayansi ayambapo kuzimvetsetsa tsopano.




## 7 Kuzungulira kwa Dzuwa

M'chaka cha 1513 Katswiri wa zanyenyezi ndi zinthu zoyandama m'malengalenga Nicholas Copernicus, adapereka mfundoyake yonena kuti dzuwa siliyenda ndipo lidangoyima malo amodzi-modzi pakati-kati pa ma pulaneti onse, ndipo mapulaneti onse amayenda kumalizungulira dzuwalo. Mfundo imeneyi idali yofalikira pakati pa Akatswiri a Sayansi ya nyenyezi kufikira mu zaka 100 zapitazo. Koma mfundo yotsimikizika ndiyakuti dzuwa silidayime malo amodzi-modzi, koma kuti nalonso likuzungulira mu njira yake yotchedwa Milky way.

> *Qur'an ikunena:*
>
> *"Ndipo Iye ndi Yemwe adalenga usiku ndi usana, dzuwa ndi mwezi; chilichonse mwa izo chikusambira mozungulira m'njira yake".*
>
> **Quran 21:33**

## 8 Mafunde a pansi pa nyanja zikulu-zikulu

Anthu ambiri ankayesa kuti mafunde a m'nyanja zikulu-zikulu amangochitika pamwamba pa madzi pokha basi. Koma Akatswiri a maphunziro a nyanja adapeza kuti pali mafunde ena amene amachitika mkati mwa madzi omwe samaoneka ndi maso koma amadziwika pogwiritsira ntchito zida zapadera-dera.

CONTENTS






Qur'an ikunena:

*"...nyanja ya madzi ochuluka yomwe yaphimbidwa ndi mafunde, ndipo pamwamba pa mafundewo pali mafundenso. Ndiponso pamwamba pake (mafundewo) pali mitambo. Ndipo mdima uwu pamwamba pa mdima uwu...".*

Quran 24:40]

Kafotokozedwe aka nkododometsa chifukwa chakuti zaka 1400 zapitazo kunalibe zida zozindikirira mafunde omwe ali pansi pa nyanja zikulu-zikulu.

## 9 Kunama ndi Kusuntha

Panali mtsogoleri wina woipa ndi wopondereza amene adakhala mu nthawi ya Mneneri Muhammad (mtendere ukhale pa Iye). Allah adavumbulutsa kwa Iye ndime iyi pofuna kumuchenjeza:

*'Ayi ndithu, ngati sasiya timukoka tsitsi la patsumba. Tsumba labodza ndiponso lamachimo'.*

Quran 96:15-16

Allah sadamutche munthu uyu kuti ngonama ayi, koma akuti tsumba lake (gawo lakutsogolo kwa ubongo wake) kuti 'labodza' ndi 'lamachimo', ndipo akumuchenjeza kuti asiye. Maufufuzi ambiri-mbiri adatulukira kuti gawo lakutsogolo kwa ubongo (frontal lobe) ndi limene limamchititsa munthu kuti aname ndi kusuntha-suntha mofuna yekha, choncho zimachititsa kuti munthu achimwe. Zinthu zimenezi zidazindikiridwa pogwiritsira ntchito chida chomwe chidapangidwa mu senchale ya makumi awiri (zaka 100 zapitazo).


## 10 Nyanja ziwiri zomwe sizilowana

Pankhani yokhudza nyanja, Mlengi wathu akuti:

*'Adaika nyanja ziwiri zokumana (ya madzi amchere, ndi yamadzi ozizira). Pakati pake pali chitsekerezo, sizilowana.'*

Quran 55:19-20

Mphamvu yapadera-dera yotchedwa 'surface tension' imatsekereza madzi a nyanja zoyandikanazi kuti asasakanikirane ndi kulowana, chifukwa cha kusiyana kwa kakhuthalidwe ka madzi awiriwa. Zili ngati kuti pali kachipupa kopyapyala kamene kali pakati pake. Zimenezi zangotulukilidwa posachedwapa ndi akatswiri owunika nyanja zikulu-zikulu.



CONTENTS






# Mwina Muhammad adaipeka Qur'aniyi?

Mneneri Muhammad (mtendere ukhale pa Iye) amadziwika mu mbiri yake kuti adali wosatha kulemba ndi kuwerenga, ndipo sadaphunzirepo phunziro lililonse lomwe likadathandizira mfundo zolondola zasayansi zomwe zili mu Qur'an.

Anthu ena amanena kuti Iye adabera Qur'aniyi kuchokera kwa ophunzira ena kapena akatswiri a Sayansi a m'nyengo yake. Ngati iye adachita kubera kapena kukopera kwa ena, ndiye kuti akadakopera limodzi ndi mfundo zolakwika za Sayansi za nthawiyo. Koma m'malo mwake Qur'an ilibe zolakwika zilizonse – kaya kumbali ya zasayansi, ngakhalenso zina zosakhala zimenezo.

Ena angathenso kunena kuti Qur'an idachita kusinthidwa pamene mfundo zatsopano za Sayansi zidatulukilidwa. Izinso sizowona chifukwa ndi zotsimikizika kuti Qur'an ndi buku lomwe lidasungidwa m'chiyankhulo chake cheni-cheni kufikira lero lino – chomwenso ndi chozizwitsa china pachoka.

# Kapena mwangozi chabe?

Ngakhale kuti kabukhuka kangofotokoza zozwitsa za Sayansi zokha, komabe pali mitundu ina yambiri ya zozizwitsa yomwe yatchulidwa m'Qur'an. Kuyambira zozizwitsa za histole (mbiri); maulosi omwe adachitikadi; maukadaulo a chiyankhulo omwe palibe angathe kupikisana nawo, osayilawanso mphamvu yomwe Qur'an ili nayo pa kusintha miyoyo ya wanthu. Zozizwitsa zonsezi sizingachitike mwangozi chabe ayi. Koma zikusonyeza poyera kuti Qur'an ndiyochokera kwa Allah, Mlengi wa ndondomeko zasayansi zonsezi. Ndi Allah mmodzi-modzi yekhayo amene adatumiza Aneneri onse ndi uthenga umodzi – kuti anthu ampembedze Allah Mmodzi, ndi kutsatira ziphunzitso za Mtumiki wake.

> *'Posachedwapa tiwaonetsa (awa okanira), zisonyezo zathu kumbali (zonse) za dziko ndi mwa iwo eni, kufikira zionekere kwa iwo kuti chimene wadza nachochi nchoona?'*
>
> **Quran 41:53**

Qur'an ndi buku la chiwongoko lomwe likutiwonetsa kuti Allah sadalenge wanthu kuti azingoyumbayumba m'dziko popanda cholinga chilichonse. Likutiphunzitsa kuti moyo wathu uli ndi tanthanuzo komanso cholinga chapamwamba zedi – (chomwe ndi:) kukhulupirira za kukwanira kwathunthu komwe Allah ali nako, ukulu wake ndi kupatulika kwake, ndikuti timugonjere.

Zili kwa aliyense wa ife kuti agwiritse ntchito nzeru ndi luntha limene Allah adatipatsa mwaulere polingalira ndi kuzindikira zisonyezo za Allah – zomwe chisonyezo chachikulu mwa izo ndi Qur'an yolemekezekayi. Werengani ndi kuzindikira kukongola ndi choonadi cha Qur'an, kuti mupeze kupambana ndi chipulumutso!

HOTLINE
+971 56 204 2045
islamicicdxb
islamicic.com  info@islamicic.com  +971 4 355 5223
DOWNLOAD CHICHEWA FLYER
www.iicdxb.com/chichewa

مركز المعلومات الإسلامي
Islamic Information Center
للتعريف بالإسلام

Part of the

# ISLAMIC e-LIBRARY

Learn more about Islam with our informative and educational materials, translated to over 50+ languages

**Quran** **Flyers** **Books**

**iicdxb.com/flyers**

**@islamicicdxb**